# *Yehova-Yire 2*

Tiyeni tikhalebe chiyimire, mphindi yokha, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

2 Atate Akumwamba, tiri oyamikira, usikuuno, chifukwa cha mwayi umene ife tiri nawo, kubweranso ku nyumba yopemphereramo, kumene ife tadzipereka tokha ndi mavuto athu kwa Inu, kuti Inu munalonjeza kuti kudzakumana ndi ife pano pansi pa Magazi okhetsedwa. Malo okhawo operekedwa omwe Mulungu anayamba wakhalapo nawo kuti wochimwa, kapena aliyense akhoze kukomana ndi Mulungu, anali pansi pa Magazi okhetsedwa. Kotero ife tikubwera mu Dzina la Ambuye Yesu, tikudziwa kuti Inu munalonjeza ngati—ngati tidzapempha chirichonse mu Dzina limenelo, izo ziyenera kuperekedwa. Ife tikukukhulupirirani Inu, Atate. Tithandizeni kusakhulupirira kwathu. Ife tikupemphera kuti kusonkhana kwathu pamodzi, usikuuno, kukhale kwa ulemelero wa Mulungu, kuti Mulungu akhoze kulemekezedwa, ndipo Dzina Lake lizindikiridwe pakati pa anthu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mwana wa Mulungu. Ameni.

Mukhoza kukhala.

3 Ndikuwutenga uwu ngati mwayi kudzakhala pano kachiwiri usikuuno, ndi kuwona gulu labwino ili la anthu lasonkhana pano. Ine ndikukhulupirira, iwo ananena kuti chinali chiwonetsero cha zinthu. Ine ndakhalapo ndi misonkhano, pafupi kwambiri, mitundu yonse ya malo kuzungulira dziko. Ine ndikukumbukira uko ku California, ine ndinali ndi misonkhano iwiri kapena itatu uko ku Cow Palace, iwo amawatcha iwo. Ndi kuyambira masaizi osiyanasiyana, kachipinda kakang'ono kokhala anthu faivi kapena sikisi, mpaka, chabwino, kusonkhana kwakukulu kumene ife tinayamba takhalapo nako pa nthawi imodzi, kunali Bombay, faivi handiredi sauzande pa kusonkhana kumodzi.

4 Koma, Bombay, chinthu chachikulu, Ambuye wathu anapulumutsako anthu ochuluka. Ngati ife tikanangokhoza kutenga mipingo kuti ikhale ndi mgwirizano, iwo akanakhoza kutenga Achihindu awo ndi ena otero. Ndipo awo anali kwenikweni, chimene ife timachitcha, "osakhulupirira." Chirichonse chimene sichimakhulupirira mwa Ambuye Yesu Khristu, ife timachitcha icho "wosakhulupirira." Ndipo uko kunali kwenikweni masauzande amene anamulandira Khristu, koma iwe ukanakhoza . . . sukanakhoza basi kufikira kwa iwo.

5 Ndiye ku Durban, South Africa, ife tinalembetsa kumeneko, anthu, sarte sauzande pa kuitanira kuguwa kumodzi, madzulo ena. Kumene, tsiku lotsatira, ameya, Sidney Smith, aku Durban,

ndi pafupifupi seveni kapena eyiti a mavani aakulu achi British amenewo anangodzadzitsidwa ndi ndodo zakale ndi zinthu zomwe anthu amayendera, kwa mahandiredi a mailosi. Kapena, iwo anawabweretsa iwo kwa masabata, kubwera kudutsa mu nkhalango, pa zonyamulira. Iwo anali atawunjikidwa onse odzaza ndi zimenezo.

6 Ameya anandiimbira ine, anati, "Upite pa zenera lako lomwe likuyang'anizana ndi Nyanja ya Indian, kunja uko ku hotelo," anati, "ndipo iwe ukawona chinachake chimene sunachiwonepo nkale lonse."

7 Ndipo apa panali mavani akuluakulu atadzadzitsamo, zomwe ife tingadzitche, ndodo ndi zonyamulira, ndi zina zotero, kuti akawanyamulire okondedwa awo kuwachotsa ku nkhalango. Ndipo anthu amene anakwera amenewo, dzulo lake, anali akuyenda kuseri kwa vaniyo, akuyimba *Kungo Khulupirira* mu chinenero chawo. Zimenezo ndithudi zinali zochitika zokondoweza kuziwona zimenezo.

8 Ndipo mmenemo munali madokotala. Ambiri a iwo anafufuza zimenezo, kuti akhale otsimikiza kuti iwo akulondola. Ife sitimafuna kufalitsa chirichonse, kapena kusindikiza chirichonse, kupatula ngati chitatsimikiziridwa, kukhala choona. Ziyenera kutsimikiziridwa!

9 Ndangolandira kumene kalata kuchokera a. . . kanthawi kapitako. Iyo inangobwera kwa ine. Ndi dokotala wapadera, wodziwika mu Indiana. Iye ndi wa Chikatolika, chikhulupiriro chake. Ndipo mwana wake ndi wansembe mu St. Meinrad monastery ku Jasper, Indiana. Uyu anali Dr. C. Ackerman. Ndipo ine ndinapezeka kuti ndinakomana naye iye pa ulendo wokasaka, kamodzi. Ndipo iye anakhala akusaka kwa zaka leveni, kufuna mbawala. Iye amalephera kuti apeze imodzi. Ndipo usiku umenewo, ife tinakhala mpaka pafupifupi thuu koloko, tikuyankhula za Ambuye.

10 Ine ndinamva dokotala uyu anali kumtunda uko ku msasa. Chotero pamene ine ndinafika kumeneko, ine ndinali kuyembekezera kuwona munthu wamwano komanso wosayanjanitsika. Koma ine ndinakomana ndi munthu wa mtundu wabwino kwambiri, wokoma. Iye anayenda akukwera, anati, "Kodi ndinu M'bale Branham?"

Ndipo ine ndinati, "Inde, bwana, ndi ineyo."

Ndipo iye anandigwira chanza. Iye anati, "Ndine Dr. Ackerman."

Ine ndinati, "Chabwino, ndithudi ndine wokondwa kukudziwani inu."

11 Ife tinayamba kuyankhula za Mulungu, ndi za momwe kuti ngati Iye anayamba wakhalapo Mulungu, Iye ayenera kukhalabe Mulungu, kapena Iye sanakhale konse Mulungu.

Mukuona? Mulungu wa mbiriyakale si wabwino lero, ngati Iye siali yemweyo kwa anthu lero monga Iye anali nthawi imeneyo.

12 Kotero, pafupifupi firii koloko, ife, oh, a—namulondola anatidzutsa ife. Ndipo anali. . .Ine ndinali kulondolera, nanenso, kotero ife timati titenge ulendo, kuwatengera amuna athu kumalo osiyanasiyana kumene ife tikanawalondolera. Panjira yopita, Dr. Ackerman anaperekedwa kwa ine.

13 Ndipo ali panjira kumeneko, iye anayima, pang'ono kusanache. Anadzayika dzanja lake pa phewa langa, anati, "M'bale Branham?"

Ine ndinati, "Inde, bwana, dokotala."

14 Iye anati, "Ndine wokhutitsidwa kwathunthu za Yesu Khristu." Iye anati, "Ine ndiri ndi mnyamata, inu mukudziwa, ndi wansembe kuno ku monastery."

Ndipo ine ndinati, "Inde, bwana."

15 Iye anati, "Ndine Mkatolika, mwa chikhulupiriro. Ine ndikuganiza ndiwo mpingowo." Iye anati, "Chabwino, ine ndikukhulupirira ngati—ngati Iye anayamba wakhalapo Mulungu, Iye ndi Mulungu wa anthu onse."

16 Ine ndinati, "Ndiko kulondola ndendende. Iye analenga anthu onse. Ndipo mwa Magazi amodzi Iye anapanga mafuko onse."

17 Ndipo iye anati, "Inde, bwana, ine ndikukhulupirira zimenezo." Anati, "Ine ndawerengapo mabuku anu." Iye anati, "Ine ndikukuuululirani izi. Ine ndikukhulupirira, ngati mutamupempha Mulungu, kuti andipatse ine mbawala lero, ine ndiyipeza iyo." Anati, "Zaka leveni ine ndakhala ndikusaka izo; ndakhala ndikugwidwa mu mkuntho wa chipale."

18 Ine ndinati, "Ine ndiwapempha Ambuye kuti akupatseni inu imodzi, dokotala. Ndizo zonse zomwe ine ndingathe kuchita." Ndipo pamene ine ndinamufunsa Iye, ndinamupempherera iye. Ine ndinati, "Dokotala, ndendende naini koloko, mmawa uno, Ambuye akukupatsani inu—mbawala yamphongo yokhala ndi nsonga faivi."

Ndipo iye anati, "Ine ndikukhulupirira zimenezo."

Ndizo zonse zimene iye ayenera kuchita. "Ngati inu mukukhulupirira izo."

19 Chotero, mzanga ndi ine, tinakwera pamwamba pa phiri, ndikumayang'ana wotchiyo. Nthawi ya 9 koloko mfuti inawombera. Iye anali ndi chimbalangondo cha nsonga faivi. Ife tinapita ndi kukamuthandizira iye kuchilowetsa icho mkati.

20 Iye amabweretsa odwala ake kuti apemphereredwe. Ine ndangolandira kumene chapadera pakali pano, kuti iye ali ndi vuto la khansa, mkazi akufa ndi khansa, iye akufuna kuti aziwulukira kuno. Koma ine ndikupita kwathu,

likadutsa mawa, likadutsa, tsiku la mkucha. Kotero ine ndinamuuza iye, ingodikirani mpaka ife tikafike kumeneko, ife tikamupempherera mkaziyo pamene ife tikafike kumeneko.

21 Chotero, onani, ambiri, ngati nkhaniyo ingakhoze kuperekedwa kwa munthuyo mwanzeru! Machiritso Auzimu apangidwa kumayankhulidwa mochuluka kwambiri, ndi kutengeka kochuluka kolumikizidwa mu izo, monga momwe zimakhalira mu china chirichonse. Mtundu—mtundu uliwonse wa chipembedzo kapena chirichonse, inu mumapeza otengeka.

22 Ngakhale mwa Achimuhamadi, inu mumapeza kuti ziripo, ndi Ahindu. Inu mumamupeza winawake pamenepo, wachinyengo wokalamba akuchitira zitsuzo alendo ena, akugona pa misomali ndi zina zotero, galasi. Koma kumbuyo mkatimo, muli munthu amene amakhulupirira kwenikweni mu zimenezo. Iye amachita zimenezo mwa nsembe.

23 Ndipo—ndipo timazipeza zimenezo mu chirichonse. Ife timapeza kutengeka. Ngakhale wotengeka wakudya amadya zochuluka kwambiri. Kapena, kapena, chirichonse!

24 Koma ngati nkhaniyo iperekedwa kwenikweni mu Lemba, ndiye palibe chomwe chingakhoze. . . Ine ndimapeza madotolo okhulupirira ochulukirapo kuposa momwe ndimapezera atumiki okhulupirira. Ine ndimatero. Ine ndimaterodi. Ochuluka amakhulupirira.

25 Ine ndafunsidwapo kwa a Mayos'. Ngati inu nonse mukuzidziwa zimenezo, izo zakhala ziri papepala lonse, ndi chirichonse. Ndi zipatala zabwino za madokotala konsekonse. Palibe kalikonse. Iwo amakhulupirira izo. Ine—ine ndakhalapo nawo madokotala obwera kudzandiuza ine, monga pa kuyankhulana kumeneko, anati, "Ife sitimadzinenera kuti ndife ochiritsa. Ife timadzinenera kuti timathandizira chirengedwe. Alipo mchiritsi mmodzi yekha; ndiye Mulungu."

26 Ndi angati anawerengapo *Reader's Digest*, ya Donny Morton wamng'ono uja, amene iwo anasaina kwa izo, "wachiritsidwa"? Ndi, "Chozizwitsa cha Donny Morton," *Reader's Digest*. Kotero, izo, izo zinandipangitsa ine kukhala pa zoyankhulana pa izo. Mnyamata wamng'ono uja analepheredwa ndi a Mayos', Hopkins, ndi onse a iwo. Ndipo Ambuye Yesu anamuchiritsa iye, anamupanga iye kukhala bwino.

27 Ndi Florence Nightingale, malemu mdzukulutuvi wa Florence Nightingale, London, England. Iye anatengedwa pandege kuchokera ku Durban, South Africa.

28 Ndipo chinthucho chanenedwa molakwitsa. Chimodzimodzi monga. . . monga nthawi zambiri mu. . .

29 Ndipo Chikhristu chimanenedwa molakwitsa kwa anthu. Chikhristu chakhala chikuperekedwa kwa anthu ngati chilengezo cha kachikhulupiriro. Chikhristu ndi Munthu

wamoyo, Yesu Khristu, Mulungu woukitsidwa, yemwe ali wamoyo ndipo ali pakati pathu tsopano. Chikhristu ndi Munthu, osati kachikhulupiriro. "Kumudziwa Iye ndi Moyo." Osati kuwadziwa nkomwe Mawu Ake; umenewo si Moyo. "Kumudziwa Iye," ndipo Iye ndi Mawu.

30 Munthu ananena kwa ine, osati kale kwambiri, iye anati . . . Ine ndinali kungokambirana za . . . zomwe ife timaganiza za Lemba lina la mu Baibulo. Munthu uyu anali wophunzira kwambiri. Iye anati, "Chabwino, inu basi simumalidziwa Baibulo lanu."

31 Ine ndinati, "Ine ndimamudziwa Mlembiyo bwino lomwe." Kotero, ndicho chinthu chofunikiracho, ngati ine ndikumudziwa Iye. Iye adzasamalira zina zonsezo. "Kumudziwa Iye ndi Moyo."

32 Ndipo, tsopano, mawa mmawa, mchipinda chino, uko, wofalitsa uthenga wanga, Dr. Lee Vayle, ali pano. Ngati muli mafunso mmalingaliro mwanu dzabwereni, iye adzawayankha iwo, adzachita chirichonse chimene iye angathe, kuti adzakuthandizeni inu. Dr. Vayle ali pano. Ine ndikukhulupirira iye ali penapake kumbuyo mchipindachi tsopano. Wophunzira wabwino kwambiri, komanso munthu wophunzitsidwa bwino pa ntchitoyo. Kotero, ngati aliyense ali ndi funso, kapena chirichonse, ndipo mmalo moyesera kuti mufunse izo pano, mu msonkhano wachigulu monga uwu, bwanji, dzamuwoneni Dr. Vayle. Iye adzakhala wokondwa kuyankhula nanu chirichonse chimene—chimene inu mungafune kuti muyankhule naye iye. Ndiyeno iye adzakhala ndi msonkhano kuno, mmawa. Ndipo ife tidzakhala okondwa ku—kukumana ndi anthu pano.

33 Ndipo, ndiye, Lamlungu mmawa kudzakhala Sande sukulu, kudutsa mu mzindawo. Ife sitiri ayi—sitikuyesetsa kuti tidzatenge Lamlungu, Lamlungu mmawa kapena Lamlungu madzulo, mu holo yoyankhuliramo kuno, chifukwa ndizo—izo sizolondola.

34 Inu mukuona, mipingo, yanu—ntchito yanu ili ku wanu—mpingo wanu. Ndipo pamene mpingo ukukhala ndi misonkhano, amenewo—amenewo ayenera azikhala malo anu. Ndipo sitikufuna kuti aliyense azichokako, pamene inu muli ndi malo anu antchito oti mukhaleko. Ngati mpingo wanu uli ndi chitsitsimutso, ndipo zikapezeka kuti talowa mu mzindawo kumene inu mukuchititsako chitsitsimutso, ife sitimatanthauza kuti tichite zimenezo, ayi nkomwe. Ife tiri kuno mu chiyanjano Chachikhristu, chololerana, kwa ubwino wa anthu onse, mipingo yonse. Ife sitiri . . .

35 Ine sindine wa bungwe lirilonse, nkomwe. Ine sindine wa bungwe lirilonse. Ine—ine basi Mkhristu. Ndipo ine, chikoka chimene ine ndiri nacho, ine ndimangoyesetsa kuti ndichigwiritse ntchito—polemekeza Khristu, ndi kubweretsa ochimwa ku kulapa. Ndipo ndizo zonse zomwe ine ndimazidziwa

kuchita kwake. Ndikuyembekezera, pa Tsiku limenelo, ndipo ndikudalira kuti Iye adzati, "Zimenezo unachita bwino." Ndipo ndiwo mawu amene ine ndikufuna ndidzawamve. . . kumumva Iye akunena.

36 Nthawi zambiri ndakhala ndikudabwa. Ine ndimakonda kumumva Iye pamene Iye anayima ndi kutambasula manja Ake tsiku limenelo, ndi kuti, "Bwerani kwa Ine, nonse inu olema ndi othodwa." Tsopano, izo zinali zakale. Koma, "Wachita bwino, mtumiki Wanga wabwino ndi wokhulupirika," izo zidzakhala zamtsogolo. Ndipo, ine, ine ndikukhala moyo kuti ndidzamve zimenezo zikunenedwa.

37 Ndipo tsopano, ndiye, Lamlungu madzulo, ife tidzapempherera odwala. Nthawizina anthu amanena za zimenezo ngati misonkhano ya machiritso. Tsopano, si msonkhano wa machiritso. Ndi pemphero la odwala. Mukuona? Ife timapempherera odwala. Ndipo, kawirikawiri, ndi pamene zinthuzo zimachitika, ndi pamene ife tikupempherera odwala.

38 Ine ndikufuna mtumiki aliyense, kudutsa mdzikoli, kuzungulira konsekonse, amene amakhulupirira, kuti abwere, mukhale otsimikiza kuti mudzabwere Lamlungu madzulo, mudzayime nafe pamene ife tidzakhale tikupempherera odwala. Mosalabadira chimene chipembedzo chanu chiri, kapena chirichonse chimene icho chiri, ife sitimasamala za zimenezo. Ndithudi, iwe umakhala ndi kumverera ndi anthu ako, ndi anthu amene ali anthu a Mulungu, ndi anthu amene akufuna kuti achiritsidwe.

39 Kumbukirani, pamene inu mwadwala, ntchito yanu yoyamba ndi kukawonana ndi dokotala ndi kuwona chimene iye ati anene. Ndiyeno ngati iye afufuza vuto la chinachake chimene—chimene iye sangakhoze; sayansi, sayansi siinakwanitse kuwululira kwa iye chithandizo chirichonse kwa inu, ndiye inu muli nawo ufulu wobwera kwa Mulungu. Iye ndiye Sing'anga wamkulu. Ndiyeno. . .

40 Ndipo kudzapemphera, ndi kudzakhala ndi pemphero likupemphereredwa pa inu. Iwo amachita zimenezo, amayenera kuchita zimenezo, mu mpingo uliwonse wa Chikhristu. Mwinamwake, iwo amatero pano. Ine sindikudziwa. Koma malo ambiri, Akhristu amapempherera odwala awo. Apresbateria ndi ochuluka a iwo akumakhala ndi misonkhano yayikulu ya machiritso kumpoto konseko, ndi madera osiyanasiyana a dziko, akupempherera odwala, ndipo akumakhala ndi zotsatira zazikulu; Apresbateria, Achilutera, Amethodisti, ambiri a iwo.

41 Chitsitsimutso chawo chachikulu chinayamba ndi misonkhano ya machiritso. Ndipo kotero iwo anachoka kwa izo, ndithudi. Gulu latsopanolo limabweramo, iwo, gulu la amuna limasonkhana pamodzi ndi kuwagawa Iwo momwe iwo akufunira kuchitira, ndiyeno pamenepo amachokapo kwa

Iwo, inu mukuona, kubwerera kumene ku kachikhulupiriro kameneko, monga Afarisi ndi Asaduki a nthawi ya Ambuye Yesu.

42 Koma tsopano, mtumiki aliyense akuitanidwa, Lamlungu madzulo, kuti adzabwere ndi kudzakhala ndi ine, ndi—ndi kudzandithandizira ine pamene tizidzapempherera odwala. Mudzatuluke nawo odwala anu ndi osautsika.

43 Tsopano, ife tikuyesetsa tsopano kuti tiwalole anthu. . .kuti tipeze ochimwa amene samawadziwa Ambuye wathu, amene samazindikira kuti Iye siali wakufa. Iye ali moyo. Iye, Iye siali wakufa. Iye ndi wamoyo kwanthawizonse. Ndipo Iye anati, "Chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo." Ndi lonjezo bwanji, ndi chitonthozo bwanji, pamene ife tikuwona nthawi ikuyandikira!

44 Akhristu onse enieni amakhulupirira kuti Kudza kwachiwiri kwa Khristu kuli pafupi. Motalikira bwanji, ife sitikudziwa. Kodi mwamuwona Alaska akukhala ndi zivomezi zina zingapo lero? Chimodzi cha izo, champhamvu monga chinachitira choyamba chija, kokha sichinagwedeze ilo pansi. Inu mukudziwa, Yesu anati zinthu za mtundu umenewo zikanadzachitika basi Kudza Kwake kusanachitike.

45 Ndipo, kumbukirani, zinthu izi zimene inu mukuziwona zikuchitika apa, Mawu ananeneratu kuti izo zikanadzakhala kuno, mofanana basi monga Iye ananeneratu za chivomezi. Chotero, pamodzi, bwanji ife osangoyika mitima yathu pamodzi, ndi kuiluka iyo mu Mawu a Mulungu, ndi kumakhulupirira ndi mitima yathu yonse? Chabwino.

46 Tsopano, usiku wathawu, ife tinali. . .Ine ndinatenga mutu wa Abraham, pamene iye anatcha dzina la Ambuye amene anawonekera kwa iye kumtunda uko pa nsembe ya mwana wake, kumene iye anali kupita. Dzinalo linatchedwa *Yehova-Yire*, ndiko kuti, "Ambuye adzadzipatsa Yekha nsembe."

47 Tsopano, usikuuno, ine ndiri ndi Malemba angapo ndi zolemba, kapena ziwiri, ndazilemba apa, zomwe ine ndikufuna kuti ndizisiye—ndizisiyire inu. Tsopano, basi ife tisanatero, tiyeni tipemphere kwa mphindi chabe, kachiwiri.

48 Atate, ife tikupemphera kuti Inu muwatenge Mawu Anu. . ."Mawu Anu ndi Choonadi." Ndipo Baibulo linati, Yesu akuyankhula, anati, "Mawu ndi Mbewu imene wofesa anafesa." Tsopano ife tikuzindikira kuti ngati mbewu ili mbewu yabwino, iyo imamera. Ndipo ngati mbewu imeneyo yachitidwa, dongosolo lake mu—mu chifuniro cha Mulungu, ndiye iyo imasiya mbewu ikumera. Ndipo pamene Yesu anali pa dziko lapansi, Iye anali Mpesa umenewo. Ndipo mbewu imene Iye anafesa anali Mawu Ake, ndipo ife tikudziwa kuti iyo imamera ndi Moyo Wake Womwe.

49 Ndipo ife tikudziwa kuti mbewu, pamene iyo igwera mu nthaka yoyenera; osati pamiyala, yopanda muzu; kapena mminga ndi nthula, zimene zingaitsamwitse iyo posakhalitsa; koma mu chikhulupiriro chabwino, cholemera, chachonde. Mbewu iliyonse idzabala mwa mtundu wake.

50 Ndipo ife tikudziwa kuti mbewu iliyonse, kapena lonjezo la Mulungu, lidzabala mwa mtundu wake, chimene iyo inalonjeza, ngati iyo igunda li-. . .nthaka yoyenera, nthaka imene yakonzedwa, yokonzekera; zonse—miyala yaponyedwa kutali, ndipo mizu, ndi kuyipidwa, ndi kudzikonda, ndi kusayanjanitsika, ndi nsanje, zonse zitakumbidwapo; muzu wa kuyipidwa umene umaphuka, umene nthawizina umawononga kwambiri chinthu chimene Mulungu akuyesera kuti achichite. Ife tikupemphera, Mulungu, kuti izo zisakhale pakati pathu, koma kuti Mawu abwino apeze malo abwino mwa awa.

51 Pamene ife tikutsatira mbadwa yaikulu iyu, Abrahamu, mu phunziro usikuuno, mulole ife tipeze malo athu, podziwa kuti ife ndife ana a Abrahamu, mwa chikhulupiriro mwa Khristu. Ndipo, ndiye, tengani ulemelero ku Dzina Lanu Lomwe ndi ulemu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

52 Ife tikhala ngati tikubwereza pang'ono pokha usikuuno, pa phunziro la zomwe ife timayankhula usiku wathawu. Izo zinali, kuti, ife tinamupeza Abrahamu kuyambira, mu Genesis mutu wa 12. Kwenikweni, dzina lake linayankhulidwa mu mutu wa 11, pamene atate wake anatsika kuchokera ku Babulo ndipo iwo anadzakhala mu—mu Uri ndipo ili. . .dziko la Akaldia.

53 Ndiyeno ife tinapeza kuti, aponso, kuti Mulungu anamuitana Abraham, munthu wamba basi dzina lake Abram. Iye anali asanakhale Abraham apabe. Ndipo, ndipo Sarah, "Sarai," Sarah sanali Sarah apabe. Kotero ife tikupeza kuti, *Sarai* ndi *Sarah* anali awiri-. . .anali maina awiri osiyana. Ndipo *Abram* ndi *Abraham* anali maina awiri osiyana.

54 Tsopano ife tikupeza kuti, mu izi, ife tinamubweretsa iye usiku wathawu, mpaka chitsimikiziro, kuti Mulungu anatsimikizira kwa iye pangano, momwe Iye akanadzatsimikizira kwa Abraham kuti Iye asunga lonjezo Lake. Izi zikupezeka mu mutu wa 15 uwu wa Genesis. Kuti momwe. . .Ndipo Abrahamu anaitanidwa cha kumadzulo, kuti abwere naye, aphe mwana wang'ombe wamphongo kapena mwana wa ng'ombe wamkazi, ndi mbuzi yaikazi, ndi nkhosa yamphongo. Ndipo ife tinalowa mu zimenezo usiku wathawu, momwe zazikazi ziwiri ndi chachimuna. Ndiyeno nkhunda ziwiri, kapena njiwa ndi nkhunda, zomwe ziri banja limodzi; ndipo tinapeza choyimira cha izo, kuti izo nthawizonse zinkaimira machiritso. Chimene, icho sichinasinthe konse. Machiritso nthawizonse akhala ali mwa chikhulupiriro. Koma

chitetezero, ndithudi, chinagawanika kuchoka ku moyo wa chinyama kupita ku moyo wa munthu.

55 Tsopano, mu Chipangano Chakale, pamene wopembedza amabwera ndi magazi. Mulungu amangokumana ndi anthu pansi pa Magazi okhetsedwa, malo okhawo amene Iye anayamba wakhalapo kapena ati adzatero konse. Iye sadzakomana nanu konse ndi kachikhulupiriro kanu. Iye sadzakumana nanu konse ndi maphunziro anu. Iye adzakomana nanu pansi pa Magazi; awo ndi malo okhawo. Israeli yense ankapembedza pansi pa magazi.

56 Ndipo ife tikupeza pamenepo ndiye, aponso, kuti ife tinapeza (chiyani?) kubwerera mu mbiriyakale ya chiyani, momwe pangano linkapangidwira ndi anthu, ndipo ife tikupeza mu nthawi ya Kummawa ndi njira zosiyanasiyana zomwe iwo amapangira pangano. Ndipo momwe ife timachitira lero, kugwirana chanza, ndi zina zotero, ndi kuti, "Tagwirizana zimenezo!" Ndipo Achijapani amaponyerana mchere pa wina ndi mzake, kukhala pangano.

57 Ndi—ndipo kuyenda kuzungulira dziko lapansi, ndipo iwe umapeza zochuluka za dziko lapansi zikadali mu chikhalidwe chomwecho chimene chinali mmasiku amenewo, makamaka Chakummawa ndi Kummawa. Baibulo lanu limadzakhala bukhu latsopano ngati mudzapite konse Kummawa, inu simudzatero konse-. . .mmbuyo mu Yerusalemu, Palestine, kumbuyo uko. Inu mudza . . .Baibulo, Ilo linalembedwa mu a . . . Ndife anthu a Chingerezi cha kuno, ndi anthu a Kumadzulo, kuyesetsa kuti amvetsetse bukhu la Chingerezi, kotero ndi chinthu chovuta kwambiri. Ngati mungabwerere kumbuyo uko, inu mukapeza ukwati ndi chirichonse, ndipo ndendende basi momwe iwo ankachitira izo mu nthawi ya Khristu. Zinthu zambiri kumeneko sizinasinthe nkomwe, mu miyambo ndi njira zawo.

58 Ndipo tsopano ife, mu izi, ife tikupeza kuti pamene iwo ankapanga pangano ili mmasiku amenewo, iwo—iwo ankajambula icho pachikopa cha nkhosa, kapena—kapena chikopa. Ndiyeno iwo ankapha nyama, ndipo ankaima pakati pa zibanthuzo. Ndi kuidula iyo, pangano lawo ili, kapena pawiri, mawu awo; ankakokerana iyo pakati, monga *choncho*. [M'bale Branham akung'amba kachidutswa ka pepala pawiri—Mkonzi]. Ndipo pamene iwo abwera pamodzi, *izi* zinkayenera kulumikizana ndendende chimodzimodzi. Zinkayenera kukumana, chidutswa ndi chidutswa, kotero izo sizimakhoza kuzembetsedwa. Kotero choncho ife tikupeza ndiye, kuti, mu phunziro lathu usiku wathawu, ife tinapeza kuti chimene Mulungu anachita kuti atsimikizire kwa Abraham pangano Lake.

59 Tsopano, Abraham, lonjezo linapangidwa kwa Abrahamu

ndi Mbewu yake pambuyo pake. Osati Abraham yekha, koma Mbewu yake. Tsopano, tsopano, mbewu, mbewu yachibadwa ya Abrahamu, inali Isaki; koma Mbewu yauzimu ya chikhulupiriro cha Abrahamu, inali Khristu. Osati kudzera mwa Isaki, dziko lonse linadalitsidwa; koma kudzera mwa Khristu, Mbewu Yachifumu, dziko lonse linadalitsidwa, pakuti Iye anafera anthu onse, mafuko onse ndi anthu onse.

60 Tsopano ife tikuwona mu izi, aponso, mu pangano ili, kuti Iye anasonyeza pamenepo chimene Iye akanati adzachite, momwe Mulungu akanati adzamung'ambe pakati Khristu Yesu. Ndipo thupilo linakwezedwa mmwamba ndipo likukhala pa dzanja lamanja la Mulungu, ndi Ufumu Mmwamba, ndipo Mzimu wa Khristu unatsitsidwa pa dziko lapansi.

61 Tsopano ngati ife tikanakhala ndi nthawi, inu mukanakhoza kutsimikizira izo. Chirichonse, gawo limodzi la Lemba linena, Ilo limapita njira yonse kudutsa mu Baibulo. Ngati Ilo silitero, ndiye—pali chinachake cholakwika. Chakale chinali mthunzi chabe wa Chatsopano, kuchitira mthunzi Icho. Ndiye, ngati inu mutenga mthunzi, inu mukhoza kudziwa bwino chomwe Chatsopano chiri. Kotero ndi kumene Iye anali, ndipo adzakhala ali.

62 Tsopano Mzimu uwu wa Khristu unabwereranso pa Mpingo, ndendende zinakwaniritsa Yohane 15 kachiwiri, kumene Iye anati, "Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi zake." Ndiyeno kachiwiri, Yohane 14:12, "Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita," ntchito zomwezo, chinthu chomwecho. Kumapitirira mmusi kudutsa Lemba! "Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu; pemphani chimene inu mufuna, icho chidzaperekedwa kwa inu." Zinthu zambiri zomwe Khristu . . .

63 "Kanthawi pang'ono ndipo dziko silindiwonanso Ine. *Dziko* lapansi," pamenepo liwu lachi Greek *kosmos*, limene limatanthauza *dongosolo la dziko*, "silindiwonanso Ine. Komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine," *Ine* puronauni ya umwini, "Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a dziko lapansi," kumupanga Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye—Iye—Iye akukhalabe. Iye anawuka kwa akufa. "Dziko, wosakhulupirira, sadzandiwonanso Ine." Iwo sadzachizindikira Icho. Koma wokhulupirira adzamuzindikira Iye, chifukwa Iye ali Yesu yemweyo yemwe Iye nthawizonse anali. Iye sanasinthe. "Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse!"

64 Ndipo tsopano, ndipo Mawu amenewo, anthu ambiri amayesera kuwapanga Iwo ngati kuti Iwo sanadzozedwe. Tsopano, ine ndikufuna kuti ndinene chinachake apa tsopano, changobwera mmalingaliro anga.

65 Ndipo ine sindimakhulupirira kuti guwa linapangidwira malo a nthabwala. Awa si malo a nthabwala. Uku ndi kuwona mtima. Ndipo pamene ife tikuwona Tsiku la Ambuye likuwonekera, ife tiyenera kukhala owona mtima mochuluka.

66 Koma panali n—nkhani anandiuza ine, nthawi ina kale, ya a—munthu wamng'ono amene. . .Uku kunali ku Boston, ndipo iye anachokapo. Iye anali ndi amayi abwino, poyamba, kuti tiyambe nkhaniyo, ndipo mayiyo ndithudi ankadziwa kuti mnyamata wake anali nako kuitana mmoyo wake, kuti azitumikira Ambuye. Ndipo izo zikhoza—izo zikhoza kuthandiza mayi aliyense, ayenera kutero, mayi weniweni aliyense, kudziwa kuti mwana wawo. . .kuti Mulungu wawalemekeza iwo ndi mwana yemwe ati azilalikira Uthenga. Icho chiyenera kukhala chofunikira pa moyo wa mayi aliyense. Ndipo kotero mayi wosaukayo, akuyesera kuti achite chirichonse chimene iye akanatha, iye anamutumiza iye kutali ku sukulu, ndi ku seminare, kuti akalandire yake—BA yake.

67 Ndipo chotero pamene iye anali kutali, amayiwo anadwalika kwambiri. Ndipo kotero iye, monga Mkhristu aliyense akanachitira, iwo anamuyitana dokotala. Ndipo dokotala. . . Iye anali ndi chibayo chapawiri. Ndipo adokotala anayesetsa zonse zomwe iye akanakhoza kumuchitira iye, kuti—kuti akayeze chibayo, ndipo panalibe kanthu. Iye anali atamupatsa iye mankhwala a—a salpha, peniselini, ndi zina zotero, kuti—kuti aphe jeremusi, ndipo izo sizinagwire ntchito. Amayiwo anadwalika kwambiri, mosalekeza. Kotero iwo anatumiza mawu kwa mwana wake wamwamuna, amene anali uko ku Asbury, Kentucky, ku Wilmore College, kuti abwere ndi kudza-. . .kudzamuwona iye chifukwa anali woti afa. Ndiyeno mmawa wotsatira, pamene mnyamatayo anali kukonzekera kuti azinyamuka, iwo analandira telegramu, "Amayi ako ali bwino kwambiri. Uzidikirira kuyitana kwina."

68 Patapita pafupifupi chaka chimodzi, mayiyo anakhala ndi mwayi womuwona mwana wake wamwamuna. Iye anabwerera kunyumba patchuthi komanso nthawi yopuma ku sukulu. Ndipo iye anati, "Amayi, ine ndinamva kuti inu munachira," iwo atatha kukhala ndi nthawi yocheza pang'ono, monga mwana ndi amayi angachitire. Anati, "Ine—ine sindinamvetse kuti ndi mankhwala ati omwe adotolo anakusinthirani, kuti achititse zanu—zikhalidwe zanu kuti zisinthe mwamsanga chomwecho."

69 Ndipo iye anati, "Mwana, izo—izo sizinali zimenezo." Iye anati, "Iwe ukudziwa kumene mishoni yaying'ono iyo ili mu msewu kuno, anthu amenewo kumusi uko amene. . . "

Anati, "Inde, ndikukumbukira zimenezo."

70 Anati, "Kuli dona ananena kuti iye anamverera kutsogozedwa kuti abwere kuno ndi kudzandifunsa ine ngati abusa angakhoze kubwera kudzandipempherera ine. Ndipo

kotero ine ndinamuuza iye kuti izo zinali zabwino." Kotero anati, "Abusawo anabwera ndipo anawerenga izo kuchokera mu Baibulo, 'Ngati wina pakati panu, wadwala, ayitane ma eledara, ndipo awadzoze iwo ndi mafuta; awapempherere iwo. Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwala.'" Ndipo anati, "Iwe ukudziwa, iye anawerenga zimenezo kuchokera mu Lemba, ndipo iye anandipempherera ine ndi kundidzoza ine ndi mafuta. Ndipo—ndipo mmawa wotsatira, ine ndinali bwino kwambiri mpaka dokotala anandilola ine kukhala tsonga. Mmasiku angapo ine ndinali bwino bwino." Chabwino, iye anatero...Anati, "Oh, Ambuye alemekezeke!" Iye anati, "Mwana, iwe uyenera kutero..."

71 Iye anati, "Amayi, inu mwayamba kuchita ngati anthu amenewo." Anati, "Tamvetserani, amayi." Anati, "Ife taphunzira ku sukulu kuti kumene iye anawerengako, Lemba lachiwiri limene iye anawerengalo linali mu Marko 16, kuti, 'Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Iwo adzaika manja pa odwala ndipo iwo adzachira,'" anati, "ife tinaphunzira uko ku sukulu kuti Marko 16, kuyambira ndime ya 9 kumapitirira, ndi yosadzozedwa." Anati, "Inu mukuona, anthu amenewo samapita ku sukulu, ambiri a iwo kumusi uko. Iwo ndi osaphunzira, mtundu wa anthu osaphunzira." Anati, "Iwo—iwo amatanthauza zabwino, sindikukaikira." Koma anati, "Ife tinaphunzira ku sukulu kuti, kuyambira ndime ya 9 kupita mtsogolo, izo zinangowonjezeredwa, mwinamwake ndi Vatican kapena chinachake, koma," anati, "chifukwa kuti gawo limenelo ndi losadzozedwa."

72 Mayi wamng'onoyo anafuula mokuwa kwambiri, "Aleluya!" Ndipo kotero iye anati...

Iye anati, "Amayi! Chabwino, ndi chiyani chakupangitsani inu kunena zimenezo?"

73 Anati, "Ine ndimangoganizira, mwana wanga, ngati Mulungu angakhoze kundichiza ine ndi Mawu osadzozedwa, kodi Iye kwenikweni angachite chiyani ndi Omwe ali odzozedwa kwenikweni?"

74 Kotero—kotero monga malonjezano enawo. "Pemphani chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho." "Ngati mudzanena kwa phiri ili, 'Sunthidwa,' ndipo osakaikira mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti chimene inu mwanenacho chikwaniritsidwa, inu mukhoza kulandira chimene inu mwanena." "Pamene inu mupemphera, khulupirirani kuti inu mulandira chimene inu mwapemphacho, ndipo izo zidzaperekedwa kwa inu." Mwaona, Iwo onse ndi odzozedwa, chidutswa chirichonse cha izo.

75 Pamene Morris Reidhead, wophunzira wabwino kwambiri, anabwera kunyumba kwanga, iye analandira ubatizo wa Mzimu Woyera; anagwa pa ka tebulo kakang'ono ka khofi mnyumbamo.

Iye anati kwa ine, anati, "M'bale Branham, ine ndamva kuti inu munali a—a . . . Ndinu wa Baptisti."

76 Ndipo ine ndinati, "Chabwino, ine ndinangodzozedwako, mpingo wa Missionary Baptist, ndiri mnyamata; sindine wa . . . "

77 Anati, "Chabwino, ndi achiyani Achipentekoste awa amene inu mukumamatirana nawowa?"

Ine ndinati, "Iwo ndi anthu basi monga inu ndi ine."

78 Iye anati, "Chabwino, tamverani," anati, "kodi inu mukuganiza kuti ndi Mzimu Woyera umene iwo ali nawo?"

Ine ndinati, "Ndithudi."

Iye anati, "Bwanji kukankha ndi kupondaponda ndi kukuwa konseko?"

79 Ine ndinati, "Chabwino, iwo ayenera kupopera nthunzi kuti ituluke mu wezulo. Ngati iwo sazigwiritsa izo ntchito, kuwapanga magudumuwo azigudubuzika." Ine ndinati, "Inu basi nthawizonse—kumangowaphunzitsa iwo za zomwe zonsezo ziri, mmalo mongoziwuzira izo mwanjira imeneyo. Muziziyika izo zizikagwira ntchito, chikhulupiriro, kunja pa msewu, kukayesetsa kuwatengera anthu mkati, mu Ufumu wa Mulungu."

80 Ndipo iye anati, "Chabwino, ine ndawawonapo iwo akuchita zonsezo." Anati, "Ine ndikuuzani inu chifukwa chimene ine ndadzera kuno." Anati, "Mnyamata wabwino wochokera ku India," anati, "iye anapeza maphunziro ake ndi sukulu." Anati, "Ine, pamene ine ndinapita kuti ndizinyamuka, ndinamutengera iye ku ndege, kuti ndikamuike iye pa ndege, kuti ndimuyambitse iye azibwerera kutsidya kwa nyanja, Ine ndinati kwa iye, ine ndinati, 'Mwana, tsopano iwe uli ndi maphunziro ako, ukubwerera kwa anthu ako . . . '" Ine ndikuganiza iye anaphunzira . . . ine sindi . . . Ine ndikuganiza zamagetsi.

81 Iye anati ndiye, anati, pamene iye anayamba kubwerera, iye anati, "Bwanji iwe suku- . . . osamusiya mneneri wakale wakufa uyo, Muhamadi, ndipo umupeze Yesu Khristu wowukitsidwa weniweni mu mtima mwako?"

Ndipo iye anati, "Bwana, ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake."

82 Tsopano kumbukirani, izi zikuchokera ku imodzi mwa masukulu akulu kwambiri a Baibulo, masukulu achikhazikitso, mnyamata uyu anali mmodzi wa aphunzitsi ake.

83 Iye anati, "Kodi Yesu wanu angandichitire chiyani ine choposa chimene mneneri wanga angachite?"

84 Iye anati, "Chabwino," iye anati, "Yesu wanga akhoza kukupatsa iwe Moyo Wamuyaya."

85 Iye anati, “Mai, Korani imalonjeza chinthu chomwecho.” Korani ndi Baibulo la Chimuhamadi, inu mukudziwa. Anati, “Ilo limalonjeza chinthu chomwecho.”

Iye anati, “Chabwino,” iye anati, “eya, ine. . . ”

86 Anati, “Iwe ukudziwa, Korani siyinalonjeze kanthu. Muhamadi sanalonjeze chirichonse koma—koma moyo pambuyo pa imfa.” Iye anati, “Yesu anakulonjezani inu aphunzitsi, kuti, ‘Zizindikiro izi ndi zodabwitsa zidzawatsatira.’” Anati, “Ndicho chimene Yesu ananena.” Ndipo iye anati, “Ife tikuyembekezera kuti tiwone zimenezo zikuchitidwa, tikuwoneni inu aphunzitsi mukupanga zimenezo.” Taganizani za zimenezo!

87 Iye anati kwa ine, “Pomwe apo,” iye anati, “Ine ndinazindikira kuti sindinakumane ndi mnyamata wausiku. Ndipo ine ndikudziwa. . .Mmodzi yemwe ankadziwa chimene iye anali kuchiyankhula.” Iye akhoza kuziziritsa izo. Koma ndiyo njira yabwino yochitira izo, kumulola mdani alumphire pa iwe nthawi imodzi monga choncho ndiyeno iwe nkusadziwa koti upite. Mukuona? Kotero iye anati, “Ine ndinazindikira kuti ameneyo sanali mnyamata wausiku.”

88 Ndipo iye anati—iye anati, “Chabwino, tsopano yang’anani apa. Yesu anauka kwa akufa.”

89 Iye anati, “Iye anatero?” Anati, “Inu mwakhala nazo zaka thuu sauzande kuti mutsimikizire zimenezo, ndipo osati nkomwe kuti magawo awiri pa atatu a dziko lapansi sanamve konse za Iye. Tsopano vuto ndi chiyani ndi anthu inu?” Iye anati, “Musiye Muhamadi adzawuke kwa akufa, ndipo dziko lonse lingadziwe zimenezo mu maora twente-foro.” Ndipo ndiko kulondola.

90 Mwaona, iwo ali ndi kavalo amayima pa manda ake. Ine ndinaziwona izo kumeneko. Iwo amasintha alonda pafupifupi maora foro aliwonse, kuyembekezera kuti iye awuka, apobe. Mwa choyimira pamenepo, kubwera pa kavalo woyera, mwaona, kuti adzagonjetse dziko lapansi.

91 Ndipo kotero iye anati, “Msiyeni—msiyeni iye adzawuke kwa akufa, ndipo dziko lonse lidzadziwa zimenezo.”

92 Iye anati, “Chabwino, Yesu anauka kwa akufa.” Iye anati, “Mneneri wanu ali mmanda.”

Iye anati, “Inu mukudziwa bwanji kuti Iye anauka kwa akufa?”

Mphunzitsi anati, “Iye ali mu mtima mwanga.”

Iye anati, “Muhamadi ali mu mtima mwanga, inenso, bwana.”

Iye anati, “Koma ine ndiri ndi chimwemwe ndi mtendere.”

93 Iye anati, “Bwana, Chimuhamadi chikhoza kubala kuwerenga maganizo kochuluka monga Chikhristu chingachitire.” Ndipo iwo amatero. Inu muyenera kuwamva iwo

akufuula ndi kukuwa. Uko nkulondola. "Kubala kuwerenga maganizo kochuluka monga Chikhristu chingachitire." Iye anati, "Chabwino, inu mukutanthauza chiyani pamene inu munanena kuti Yesu analonjeza zinthu zonsezi kwa inu?" Anati, "Ine ndikuganiza kuti inu mukunena za Marko 16?"

Iye anati, "Inde, ndi chimodzi mwa izo. Osati zonse, koma ndi chimodzi."

94 "Yesu anati, Mawu otsiriza amene Iye ananena kwa Mpingo Wake, 'Pitani inu mdziko lonse, mwaona, ndipo kalalikireni Uthenga, ndipo zizindikiro izi zidzamutsata wokhulupirira.' Mpaka liti? 'Dziko lapansi lonse; cholengedwa chirichonse. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.' Mawu otsiriza amene Iye ananena, molingana ndi Lemba lanu."

95 Iye anati, "Chabwino, inu mwaona," anati, "ndizo basi . . . " Anati, "Inu mwaona, gawo limenelo si lodzozedwa." Anati, "Iye kwenikweni sanali kutanthauza zimenezo. Izo sizinali . . . "

96 Iye anati, "Izo si zodzozedwa?" Anati, "Kodi ndi mtundu wanji wa Bukhu lomwe inu mukuwerenga?" Anati, "Korani yonse ndi yodzozedwa." Hmm! Ndiko kugonja kwa kufooka kwa fioloje, fioloje yopangidwa ndi munthu yomwe ilibe—Mzimu kuti uyimirire ndi kuyang'anizana ndi chinthucho.

97 Monga ana Achihebri anati, "Mulungu wathu ndi wokhoza kutilanditsa ife mu ng'anjo yamoto iyi, komabe ife sitigwadira fano ili." Ife tikusowa anthu olimba mtima. Munthu amene wakhulupirira Mulungu nthawizonse wakhala wolimba mtima ndipo amakhulupirira mu zauzimu. Munthu amene amakhulupirira Mulungu!

98 Bambo Reidhead anati, "Ine ndinamenyetsa pansi, M'bale Branham, ndinamenya fumbi monga *choncho*, ndipo ine sindinathe kumuyankha munthuyo." Iye anati, "Ine ndinatsimikiza mu mtima mwanga kuti ndibwere kudzakuwonani inu pambuyo pa zimenezo, ndi kudzafunsa kuti izi zinali za chiyani." Ndipo anati, "Pano ine ndiri." Iye anati, "Ngati Mzimu Woyera . . . "

99 Anati, "M'bale Branham, amayi anga ananditumiza ine ku sukulu." Ndipo anati, "Ine, pamene ine ndinapeza BA yanga, ine ndinaganiza kuti ndi zimenezo ndendende . . . "

Ine ndinati, "Ine ndikudziwa chimene inu mukutanthauza."

100 Anati, "Ndiye tsiku lina ine ndinapeza BA yanga, ine ndinaganiza pomwe apo ine ndamupeza Khristu. Iye kunalibeko kumeneko pamene ndimapeza Digiri yanga ya Udokotala." Anati, "Ine ndiri nawo madigiri okwanira, madigiri aulemu, kuti ndimate makoma anu, ndipo Khristu ali kuti mu zonse zimenezo?"

101 Ine ndinati, “Ndine ndani kuti ndinene kuti aphunzitsi akulakwitsa? Koma izo si zimene ife tikuzikamba. Ndi Munthuyo, Khristu, yemwe inu muyenera kumudziwa.”

102 Tsopano bamboyo akuchita misonkhano yayikulu konsekonse. Ndipo Doctor Lee Vayle apo, mzanga wabwino wa ine, ndi mzake wa iye, nayenso. Ndipo iye akuchita bwino kwambiri, akupempherera odwala ndipo akukhala ndi misonkhano yokopa anthu yaikulu ndi chirichonse. Ndi chifukwa chakuti mwamunayo anakhulupirira.

103 Tsopano, taonani, Mzimu umene unali mwa Khristu, thupi, Yesu yemwe anali Mulungu, Emanuele, Mzimu Woyera, Mulungu, unadzatsika mwa Khristu, ndipo Iye anapangidwa “Mulungu nafe.” Ndiyeno Iye anali . . . Uko kunali kudzatiwombola ife; Magazi Ake anakhetsedwa.

104 Tsopano, mu Chipangano Chakale, pamene wopembedza akabwera ndi kudzaika manja ake pa chopereka chake, ndipo iye nkudula khosi la . . . wansembe ankatero, kapena kupereka nsembe. Wopembedzayo ankagwira nsembeyo ndi manja ake, ndi kumamverera a—misozi ya mthupi, ndipo kamwana ka nkhosa kakufa; ubweya wake wawung’ono ukusambitsidwa ndi magazi ake, paliponse mmanja a wokhulupirira, ndi zina zotero, wagwidwa mu mphamvu, kuti awotchedwe pamenepo pa guwa. Wokhulupirirayo amazindikira kuti iye amayenera kukhala wofera tchimolo, koma mwanawankhosa anali kufa mmalo mwake. Tsopano, koma moyo umene unali mmagazi amenewo, sukanakhoza kubwereranso pa wopembedza, chifukwa iwo anali magazi a chinyama, amene alibe solo. Koma mu . . . Chotero pamakhala chikumbutso cha tchimo, mosalekeza.

105 Koma, tsopano, Yesu pokhala Emanuele, ndiye Moyo wa Mulungu unali mwa Iye, ndipo uwo umabwerereranso; osati Moyo wa munthu wokha, koma Mulungu Mwiniwake, mmawonekedwe a Mzimu Woyera, umabwerera ndi kudzakupangani inu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Zikatero inu mumakhala ana aamuna ndi aakazi. Ndiyeno pamene iwe umverera kung’ambidwako, ndi masautso ndi chilango chimene Yesu anadutsamo, kunyozedwa, utumiki Wake kutchedwa ntchito ya mdierekezi, “Belezebule,” ndipo kusekedwa, ndi kunyozedwa, ndi atsogoleri achipembedzo, ndi kukanidwa. “Iye anabwera kwa Ake Omwe; Ake Omwe sanamulandire Iye.” Ndi zinthu zomwe Iye anadutsamo nazo! Ndiyeno kuti apereke moyo Wake nsembe pa mtanda, kuti adzawombole icho chimene Mulungu anachidziwiratu. Kuwombola; kulibweretsa ilo pamalo amene ilo—ilo linagwerapo. Ndiye, Mulungu anachita zimenezo polinga kuti adzatumizenso Mzimu Woyera pa Mpingo tsopano, kuti Iwo . . . anthu, okhulupirira. Ndi wa okhulupirira okha.

106 Iwo si wa osakhulupirira. Iwo sadzawuwona konse iwo. Iwo ndi akufa, kuyamba ndi kuyamba.

107 Tayang'anani pa Afarisi amenewo pamene iwo anamuwona Yesu akuchita chizindikiro chimene chimayenera kukhala chizindikiro cha Umesiya.

108 Tayang'anani pa Petro, iye anakhulupirira izo tsopano. Ndipo Nataniele anakhulupirira izo pakali pano. Mkazi wa pa chitsime anakhulupirira izo; Bartimeyu wakhungu. Onse amene analandira izo, anakhulupirira izo.

109 Koma atsogoleri amenewo anayima pamenepo ndipo anati, "Ndi Belezebule, mzimu woyipa, mtundu wina wamatsenga kapena chinyengo."

110 Yesu anati, "Inu mukanena zimenezo motsutsa Ine, Ine ndikukhululukirani inu," nsembe inali isanapangidwe, "koma pamene Mzimu Woyera udzabwera kudzachita chinthu chomwecho, mawu amodzi otsutsa Iwo sadzakhululukidwa mdziko lino lapansi ngakhale mdziko likudzalo."

111 Chifukwa chiyani iwo sanakhulupirire izo? Yesu anati "Inu ndinu ochokera kwa atate wanu mdierekezi, ndipo ntchito zake inu mudzazichita." Uko nkulondola.

112 Kuwakhulupirira Mawu, ndi kuwalandira Mawu ndi kuwalola Iwo akhale Moyo. Tsopano, Mulungu akusonyeza pamenepo momwe Iye anali kutsimikizira pangano ili. Izo ziyenera kukhala mwanjira imeneyo. Mpingo! Osati bungwe, osati chipembedzo; koma munthu payekha ndi Mulungu ayenera kukhala Mzimu womwewo. Ndicho chinali cholinga cha Mulungu, pachiyambi.

113 Adamu ndi Eva anali mzimu womwewo. Baibulo linanena mu Genesis, mu 1:27, "Mu chifanizo cha Mulungu . . . " Mulungu ndi Mzimu. "Mu chifanizo cha Mulungu anamulenga Iye mwamunayo; mwamuna ndi mkazi Iye anawalenga iwo," mmawonekedwe a mzimu umene unali mwa Mulungu. Ndipo Adamu anali woti adzasamalira za—za nthakayo, monga momwe Mzimu Woyera ukuyenera kutsogolera Mpingo tsopano. Ndipo, komabe, munthu sanali mu thupi, ndipo iye anali zonse chachimuna ndiponso iye anali wachikazi, chifukwa ndi mzimu womwe womwewo.

114 Ndiye Mulungu anamulenga munthu kuchokera ku fumbi la dziko lapansi, ndipo anamupanga iye mmawonekedwe a chinyama. Chimene, ife tsopano ndife chinyama, ife tikudziwa. Ndife—ndife chinyama. Ndipo ndicho chinyama chamagazi ofunda, ndipo ife tiri mu chifaniziro chimenecho cha moyo wa chinyama.

115 Ndipo kenako Mulungu anatenga nthiti kuchokera kwa Adamu, osati a . . . Mkazi ndi wochokera kwa mwamuna, osati ndendende mu chirengedwe chapachiyambi. Iye anatenga nthiti.

Iye analekanitsa chathupi, ndipo anatenga mzimu wachikazi kuchokera mwa Adamu ndipo anawuyika iwo mwa Eva. Apo panali mwamuna ndi mkazi.

116 Ndipo pamene iwo anatuluka mmalo amenewo, iwo anachoka mu chikhalidwe chawo choyenera. Panali kupotoza penapake. Pamene mkazi akufuna kukhala wachimuna, kapena a—kapena a—kapena mwamuna kufuna kuchita mwachikazi, pali chinachake cholakwika penapake. Iwo achoka pamakhalidwe awo oyenera.

117 Ife tikuzizindikira izi mwa Rebekah ndi—ndi Isaki, pokhala wachibale wake wa magazi, mwaona, koma tsopano izo zinali kuyimira mbewu yachibadwa ya Israeli. Koma, mwa chikhulupiriro, Khristu anabwera powonekera, chimene sichiri mwachibadwa.

118 Monga chizindikiro chimakhala pa, magazi pa mphuthu ya chitseko, uko mu Igupto. Ziribe kanthu kuchuluka kwa mdulidwe, kuchuluka kwa pangano limene iwo anali nalo, chizindikiro chinkayenera kuti chiwonetsedwe kapena pangano limathetsedwa. Ndithudi. "Pamene Ine ndiwona magazi, Ine ndidzadutsa pa inu."

119 Tsopano chizindikiro si Magazi; ndi Moyo umene unali mu Magazi, Mzimu Woyera. Ndipo ndicho. . .Ine sindikusamala momwe inu muliri wachipembedzo; kupatula ngati inu mulandira Mzimu Woyera, inu mudzawonongeka. Ndiyo njira yokhayo. Palibe Lemba lina loti lichite kalikonse, kokha ilo lokha. "Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiwombolo chanu," Aefeso 4:30.

120 Zindikirani tsopano, ife tikubwerera, ndiye izo zikusonyeza kuti Adamu ndi Eva anali mmodzi, kuyamba ndi kuyamba. Mwamuna ndi mkazi akuyenera kukhalabe mmodzi.

121 Tsopano, koma pamene iwo analekana, ndiye, kulowa mu thupi, panali pamenepo pamene Eva anagwa. Kugwa! Chifukwa chiyani? Ku kusakhulupirira Mawu, gawo lirilonse la Iwo. Anthu ena akhoza kutenga gawo limodzi la Mawu, koma osati enawo. Zonsezo ziyenera kukhala pamenepo. Mukuona? Mukuona? Iye anangokaikira gawo limodzi la Iwo. Ndipo ngati matenda onse awa ndi mavuto omwe ife takhala nawo tsopano anabwera ndi mkazi mmodzi kukaikira gawo limodzi la Iwo, kodi ife tidzabweza bwanji chirichonse kuposa kukhulupirira Iwo onse, ndi kuwavomereza Iwo onse? Iwo anali awo. . .Iwo analimbitsidwa ndi Mawu amenewo. Pamene iwo analekanitsidwa, mu thupi, iwo anagwa. Iye anagwa, mwa Mawu. Iye. . .Penyani, kodi iye ankafunafuna chiyani?

122 Basi anthu ambiri lero, akufuna njira yabwinoko, yamasitailo, njira yophweka. Iwo samafuna kuyang'anizana nacho chinthu chimene chayikidwa patsogolo pawo. Ngati

iwo atero, iwo amachotsedwa mu gulu lawo, kuchotsedwa, amaganiziridwa mochepa.

123 Kodi inu simukudziwa, kuti, “Anthu onse adzayankhula zoipa za inu, monama, chifukwa cha Ine. Sangalalani ndipo mukhale okondwa mopitirira, pakuti mphotho yanu ndi yaikulu Kumwamba, pakuti kotero anazunza iwo aneneri amene anakhala pambuyo pa inu. Ndipo onse amene amakhala mwaumulungu mwa Khristu Yesu adzavutika ndi mazunzo.”

124 Tsopano ndi chiyani chinanso chimene ife tikufuna kuti Iye anene? Masauzande a Mawu ife tikanakhoza, Malemba, okhudzana ndi zimenezo, adzayenda kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso.

125 Kuti chirichonse chimene ife tiri nacho lero, chinayambira mu Genesis. Ndi gawo la mbewu. Kusakhulupirira konse ndi chirichonse chinayambira pomwe apa. Mpingo unayambira pomwepo. Chirichonse chinayambira pamenepo. Ziri ngati mipesa iwiri ikukula, ndipo umodzi kumatsanzira umzake, ndi kumafika mofanana pafupifupi chimodzimodzi.

126 Monga Moabu komanso Mose. Apo panabwera Israeli, wamng’ono, wopanda chipembedzo, wopanda fuko nkomwe. Ndipo iwo anali nayo nsembe yomweyo kuno mu Moabu; chipembedzo chabwino, olemekezeka awo onse anatulukako, anapereka nsembe yomweyo. Kuyesera kutero. . . Bishopu wawo kumtunda uko, Balaamu, anabwera kumeneko kuti adzatemberere chimene Mulungu anali atachidalitsa. Iwo anaganiza, “Anthu opanduka awa! Iwo alibe nkomwe nyumba ya tchalitchi, monga izo zinkakhalira. Iwo anali amwendamnjira basi.”

127 Ndipo Iye anati, “Koma iwo analephera kumva mfuu wa Mfumu mu msasamo. Iye analephera kuti awone machiritso Auzimu awo akupita pamenepo, pogwiritsa ntchito serpenti imeneyo. Ndi Thanthwe lokanthidwa, kuwapatsa iwo moyo! Kufuula kwa Mfumu mu msasa!”

128 Iye analephera kuwawona Iwo, bishopu wochititsidwa khungu uja. Koma apobe, mwachikhazikitso, iye amalondola chimodzimodzi monga Mose anali; maguwa seveni, nsembe seveni, anapereka ngakhale nkhosa yamphongo, kuyankhula za kudza kwa Khristu.

129 Koma Mulungu samasowa aliyense kuti amutanthauzire Iye. Iye ndi Wodzitanthauzira Yekha. Iye amapanga lonjezo, kenako Iye amalikwaniritsa ilo, ndipo ndiko kutanthauzira kwa ilo. Palibe amene ayenera kutanthauzira izo. Mulungu samafunsa aliyense. “Baibulo ndi lopanda kutanthauzira kwa mseri.” Aliyense akuyesera kunena kuti Iwo akutanthauza *ichi*, *icho*. Mulole Mulungu aziyankhulire Yekha. Iye ndi Mmodzi yemwe amachita izo. Iye anapanga lonjezo; Iye amayima kumbuyo kwa ilo. Iye amatero, kwa okhulupirira.

130 Koma osakhulupirira samalandira kanthu. Izo si za iwo. Iwo ndi akufa, kuyamba ndi kuyamba. Iwo sanaimiridwe nkomwe. Mulibemo kalikonse mwa iwo. Iwo ndi makoko akufa. Inu simukufuna kukhala monga chomwecho.

"Dzazidwani ndi Mzimu!"

131 Zindikirani, Iye analekanitsa Eva ndi Adamu, ndipo iye anagwa. Adamu anapita ndi iye. Tsopano, "Adamu sananyengedwe." Eva ananyengedwa. Koma Adamu, Adamu woyamba, analimwana wa Mulungu nayenso. Ndipo iye anatuluka chifukwa cha chikondi cha Eva, kuti ayesere kumubweretsanso iye, chifukwa iye ankamukonda iye.

132 Khristu anachita chinthu chomwecho, kuti amuwombole Iye abwerere. Ku chiyani? Mawu. Nchiyani chinayambitsa kugwako? Mawu, kusakhulupirira Mawu, Mawu onse. Ndipo Khristu anabwera kuti Iye adzakhoze kukhala mmodzi wa ife, Moyo Wake mwa ife, kuti adzapitirize Mawu. "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Mulungu yemweyo! Ndi chifukwa chake Iye anabwera, kuti adzachite zimenezo.

133 Tsopano ife tikupeza, mu chitsimikiziro, kutiwombola ife kubwerera kwa Iyemwini, kuwombola ana obwerera mmbuyo amene anasokera mnyumba yosungiramo mitembo iyi; ndi kubwerera ku Mawu kachiwiri, kubwerera ku Mawu ozindikiritsidwa!

134 Tsopano Ayuda amenewo, pamene Yesu anabwera, iwo ankakhoza kunena, "Ife tiri nawo Mawu. Ife tiri nawo Mawu. *Apa* pali zimene Mose ananena. Ndife ophunzira a Mose." Yesu, wa zaka thwelovu zokha zakubadwa, amatsutsana nawo iwo. Ndiyeno pamene . . . Mwaona, ndicho chimene munthu amachita kwa Iwo.

135 Koma Yesu anati, "Ngati Ine sindichita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Pakuti, ntchito zimene Atate andipatsa Ine kuti ndizichita, izo zimachitira umboni Yemwe Ine ndiri."

136 Ndani? Munthu aliyense amene anatumidwa ndi Mulungu, Mulungu amachitira umboni ku ntchito zimene Iye anamudzozera iye kuti adzachite. Ngati izo sizitero, Lemba silikuikira kumbuyo izo, zisiyeni izo zokha.

137 Ngakhale mu Chipangano Chakale, iwo anali ndi njira yodziwira ngati izo zinali zoona kapena ayi. Iwo ankawatengera iwo kumeneko, wolota, kapena—kapena wolosera, kapena yense yemwe iye anali, ankawatengera iwo ku Urimu Tumimu. Uko kunali Kuwala kwauzimu.

138 Mulungu nthawizonse ndi wauzimu, amagwira ntchito mu zauzimu. Malingana ngati alipo Mulungu pamenepo, chiripo chauzimu, ngati ali Yehova Mulungu.

139 Ndipo, pamene, ziribe kanthu momwe loto likumvekera bwino, ngati ilo silinanyezimirire pa Urimu Tumimu ameneyo, ndiye ilo ndi lolakwika.

140 Tsopano unsembe wakale wa Aroni unathetsedwa, komabe ife tiri ndi Urimu Tumimu. Ili ndi vumbulutso la Yesu Khristu, likumuwulula Iye mu Mawu awa. Ndipo chirichonse chimene chiri chotsutsana ndi Mawu amenewo si Mulungu; motsutsana ndi Iwo. Koma Mulungu amadziyankhulira Yekha. Iye amadzizindikiritsa Yekha ndi Mawu Ake.

Ndi pamene Yesu anamugonjetsa Satana. "Kwalembedwa . . . "

141 Ndiye apa panabwera Satana akubwerera, ndipo anakwawira mkati kachiwiri. Iye anati, "Inde, kwalembedwanso . . . " Koma nthawi imeneyo, pamene iye anabwera, iye anagunda a—mphamvu yamagetsi yamphamvu. Nthawi imeneyo inayimba mapiko ake. Iye analumpha kuchoka pamenepo, ndiye.

142 Iye anati, "Kwalembedwa, 'Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse otuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.' Pita iwe kumbuyo Kwanga, Satana!" Mukuona?

143 Taonani zimene zinachitika. Mulungu nthawizonse wakhala akudzizindikiritsa Yekha mwa Mawu Ake olonjezedwa. Tsopano ngati Afarisi amenewo akanayang'ana mmbuyo momwe, Mose anati, "Ambuye Mulungu wanu adzautsa Mneneri wonga ine." Izo zinali mu Lemba.

144 Koma ndi zosadabwitsa kuti Yesu anawathokoza Atate, anati, "Ine ndikukuthokozani Inu, Atate, Inu mwabisa Izi kwa maso a anzeru ndi aluntha, mwaziululira Izo kwa makanda omwe angati aphunzire."

145 Pamene Iye ananena kwa Petro pa tsiku limenelo, pamene iwo anabwera uko. Pamene Iye anati, "Kodi munthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?"

146 "Mmodzi wa iwo amati Ndinu 'Eliya,' ndipo wina amati Ndinu 'Mose,' ndi zina zotero."

Iye anati, "Koma ilo si funsolo. Ine ndakufunsani inu."

Anati, "Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo."

147 Iye anati, "Wodala ndiwe Simoni, mwana wa Yona, thupi ndi mwazi sizinawululire izi kwa iwe. Sunaziphunzire konse izi mu seminare, palibe amene anakuphunzitsa izi, koma ndi vumbulutso." Oh, mai! "Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo

Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzakhoza kuwulaka Iwo," vumbulutso, kapena chizindikiritso cha Yesu Khristu.

Iye anati, "Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, musandikhulupirire Ine."

148 Tsopano tiyeni tipitirize ulendo. Ife tikumupeza Iye. . . Tsopano tiyeni tipite ku mutu wa 17. Ife tikumupeza Iye apa mu mutu wa 17, kumene Iye anawonekera kwa Abrahamu pambuyo pa kutsimikizira kwa ichi, kusonyeza chimene Iye akanati adzachite.

149 Ndipo tsopano, kumbukirani, Mzimu umabwera pa. . . Ndipo Mzimu umene uli mu Mpingo, Mpingo weniweniwo, Mpingo woona, Mpingo wa Mulungu, anthu a Mulungu; Mzimu umene uli mwa iwo, uli pa, Mzimu womwewo uli pa Khristu, ndi lonjezo, "Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita."

150 Kumbukirani, nthawi ina mu kupachikidwa, basi izo zisanachite, iwo anamuveka chinsanza pa nkhope Yake, ndipo anamumenya Iye pamutu, ndi bango, anati, "Tsopano ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, izo. . . Ndiwe—Ndiwe mneneri, iwo akundiuza ine. Losera, mneneri!" Iwo anapatsirana ndodoyo, "Tiuzeni ife amene wakumenya Iwe." Mukumuwona mdierekezi ameneyo? Mukuona?

151 Iye anati, "Ine ndamva kuti Ndiwe wochita zozizwitsa. Sandutsa miyala iyi ikhale mkate. Undirole ndikuwone Iwe ukuchita zimenezo. Ine ndidza—ine ndidza—ine ndikukhulupirira Iwe ngati Iwe uti uchite zimenezo monga chomwecho, kusandutsa miyala iyi kukhala mkate. Ine ndikukhulupirira. Ine ndichita zimenezo."

152 Munthu anandiuza ine osati kale litali, anati, "Ngati inu mungakhoze kutulutsa munthu mmodzi yemwe wachiritsidwa, ndi cholemba cha dokotala!"

153 Ine ndinati, "Oh, chifundo, bambo, khalani chete. Kwa ubwino!" Ine ndinati, "Ine ndibweretsa madokotala mwa mahandiredi."

Iye anati, "Ine ndiri ndi madola masauzande akukuyembekezerani inu, ngati inu mutero."

154 Ndipo ine ndinabweretsa madokotala, ndi nkhanizo. Iye anati, "Chabwino, ndalama ziri mu. . . "

155 Ine ndinati, "Ndikufuna ndalama imeneyo ya chopereka chaumishonare." Ndipo iye anati. . . "Mutumizeniwinawake amene amakhulupirira Uthenga, kutsidya kwa nyanja."

156 Iye anati, "Chabwino, ndiroleni ine ndimtenge mtsikana wamng'ono, ndipo ine ndi abale anga tiyime mozungulira, ndipo ife timudula dzanja lake, ndiyeno inu muchize ilo pomwe pano pamaso pathu, ndipo ife tikukukhulupirirani inu."

157 Ine ndinati, "Inu mukusoweka kuchiritsidwa m'maganizo." Ndiko kulondola ndendende. Munthu wogwidwa ndi mdierekezi kwambiri!

158 Mmodzi yemweyo anati, "Ngati Inu muli Mwana wa Mulungu, ngati Inu muli, tsikani pa mtandapo." Oh, pamene Baibulo lomwelo linanena kuti Iye anayenera kupachikidwa pa mtanda!

159 Kayafa anati, "Iye anapulumutsa ena; Iyeyekha Iye sangakhoze kudzipulumutsa." Osadziwa kuti kumeneko zimenezo, koma kuyamikira kwakukulu kunayamba kwaperekedwapo kwa Iye. Ngati Iye akanadzipulumutsa Yekha, Iye sakanakhoza kupulumutsa ena. Iye ankayenera kuti adzipereke Yekha.

160 Ndithudi, Iye anadziwa yemwe anamumenya Iye, koma Iye samamuchitira chisudzo mdierekezi. Mulungu si wa chisudzo. Iye samachitira chisudzo mdierekezi. Ntchito zake zimatumizidwa kwa iwo amene akhulupirira, osati kuti azingochita mowonetsera.

161 Zindikirani, Iye anawonekera kwa iye apa pamene iye anali usinkhu wa zaka nainte ndi naini, ndipo Iye anawonekera kwa iye mu dzina la Mulungu Wamphamvuzonse. Dzina pamenepo, mu Chihebri, ndi *El Shaddai*.

162 Tsopano, Mulungu ali nawo maina a pawiri seveni, achiwombolo. Ife tikudziwa zimenezo. Ndipo inu simungakhoze kuwalekanitsa iwo kwa Khristu. Inu simungakhoze kuwalekanitsa iwo. Khristu anakumana nalo limodzi lirilonse la pawiri limenelo, maina achiwombolo. Inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Iye, kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ndi Yehova-Yire, "nsembe yoperekedwa ya Ambuye"? ["Ameni."] Ndiye nanga bwanji *Yehova-Rafa*, "Ambuye amachiza matenda anu onse"? ["Ameni."] Ndipo ngati izo sizinaikidwe kwa Khristu, ndiye Iye sanali Yehova-Yire. Kotero inu simungakhoze kuzilekanitsa izo, chinthu chonsecho nchomangirizika, ndipo ndi zimenezotu. Iye sangakhale Yehova-Rafa popanda kukhala Yehova-Yire, komanso Iye sangakhale Yehova-Yire popanda kukhala Yehova-Rafa. "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa." Palibe kutsutsana za Zimenezo.

163 Tsopano ife tikupeza apa, Iye akuwonekera mu dzina la El *Shaddai*, "Wamphamvuzonse." A . . . Kwenikweni, liwulo, liwu la Chihebri *shad*, s-h-a-d, ena amalitchula ilo "mthunzi." *Shad* amatanthauza "bere," ngati bere la mkazi. Ndipo Iye anawonekera kwa iye mu dzina la El Shaddai, lomwe liri mu zambiri, *wamabere*. "Ine ndine Mulungu wa Mabere. Abrahamu, zaka nainte-naini zakubadwa, yenda pamaso Panga! Ukhale wangwiro, ukhulupirire Mawu Anga! Uzingopitirira

kumakhulupirirabe! Ine ndinalonjeza, pa sevente-faivi; ndi izi apa, zakhala—zakhala ziri zaka twente-foro tsopano chiyambireni pamene Ine ndinakupangani inu lonjezo." Ndipo chotani—chitonthozo chotani icho chikanayenera kukhala kwa mwamuna wokalamba, wausinkhu wa zaka nainte-naini. Ndipo mphamvu zake zonse zinatha, ndipo apa Mulungu anayima pamaso pake, anati, "Ndine El Shaddai. Ine ndine Mulungu wa Mabere." Ameni. "Yamwa mphamvu zako kuchokera kwa Ine. Ine ndine mphamvu zako."

164 Monga, monga Chipangano Chatsopano ndi Chakale, Mulungu Wamabere. "Ine ndine Mulungu wa Mabere, yamwa mphamvu zako kuchokera kwa Ine."

165 Monga mwana wamng'ono pamene iye akudwala, akudandaula; wadwala, wafooka, iye amatsamira pa bere la amayi ake ndipo amayamwa mphamvu zake kuchokera kwa mayiyo. Mwakuyankhula kwina, "Abrahamu, sindiwe kanthu koma khanda kwa Ine." Zaka nainte-naini zakubadwa, sizinakhale nthawi iliyonse, moyo wake.

166 Ingokumbukirani, Yesu anapachikidwa, monga dzulo. Zaka sauzande padziko lapansi—padziko lapansi, ndi tsiku limodzi ndi Mulungu. Mwaona, basi monga Iye anapachikidwa dzulo.

167 Ndipo zindikirani, "Ndine El Shaddai. Ndiwe mwana wamng'ono, wofooka. Koma tsamira pa chifuwa Changa, lonjezo Langa, ndipo uyamwe kuchokera kwa Ine mphamvu zako. Ine ndine mlengi amene anapachika miyamba ndi dziko lapansi, anayika nyenyezi kutaliko. Kodi pali chirichonse chachikulu kwambiri kwa Mulungu? Ndine El Shaddai, ndipo iwe ndiwe mwana Wanga. Ngakhale iwe uli wofooka, ndipo Ine ndikukulola iwe ukhale mwanjira imeneyo kuti ndiwone chomwe uti uchite nazo izo. Ine ndidzapanga chitsanzo kwa anthu mtsogolo, munthu ameneyo akadzakhulupirira Mawu Anga. Ine ndidzaima nawo Iwo. Ziribe kanthu zomwe zingatengere, motalika bwanji, Ine ndidzachita icho. Ine ndidzayima ndi Iwo. El Shaddai! Yamwa mphamvu zako kuchokera kwa Ine."

Oh, inu mukuti, "Ngati ine ndingakhulupirire . . . "

168 Iye akadali El Shaddai. Iye akadali Mulungu Wamabere, Chipangano Chatsopano ndi Chakale. Yamwa mphamvu zako kuchokera kwa Iwo, oh, chirichonse chimene iwe ukuchisowa. Mwanayo, iye alibe thandizo, ayenera kuchotsa mphamvu zake kuchokera kwa amayi ake; ndiyo njira yokhayo imene iye angapezere mphamvu zake. Ndiyo njira yokhayo wokhulupirira angakhoze kupezera mphamvu zake, ndi kuzikoka izo kuchokera ku Mawu a Mulungu. Ndiyo mphamvu yake, malonjezo a Mulungu kwa iye. Kuima pamenepo ndi kuwakhulupirira Iwo!

169 Ndipo osati kokha mwana wamng'ono pano akuimiridwa pamene akudwala, iye akudandaula, amayi akhoza kumuyika iye ku lake—bere lake, ndipo iye amapita kukayamwitsa mphamvu zake; iye amakhutitsidwa pamene iye akuyamwa.

170 Umo ndi mmene zimakhalira ndi mwana weniweni wa Mulungu. Ziribe kanthu zomwe wokayikira anena, chirichonse chimene iye akukhulupirira. Ngati inu mukuwakhulupirira Iwo moona, Yesu sangakhoze kunama. Inu mwakhutitsidwa kuti Iwo awululidwa kwa inu. Inu muli nalo lonjezo, ndipo palibe chimene chiti chidzalepheretse ilo. "Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga," mwaona, auzimu, Mawu owululidwa a Choonadi.

171 Pamene mukuyembekezera, mukupumulira mu chikhulupiriro chanu, mutenge lonjezo la Mulungu. "Ine ndikukukhulupiririrani Inu, Ambuye. Inu munalonjeza kuti mudzandipatsa ine ubatizo wa Mzimu. Ine ndikupumula mu Chanu. . .mu chikhulupiriro. Chikhulupiriro changa chimene ine ndiri nacho mwa Inu, ine ndikuyamwa kuchokera ku gwero langa, pakuti gwero langa, kuchokera—kuchokera. . .kwa thanzi langa, kuchokera ku gwero Lanu, Mawu.

172 "Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma kuchokera pachifuwa cha Mulungu iye adzayamwitsa mphamvu yake." Mawu aliwonse amene amachokera mkamwa mwa Mulungu, iye adzalandira mphamvu yake pamene Iye akuchokera mwa—mkamwa mwa Mulungu, Mawu.

173 Monga Abrahamu, Abrahamu anali akupumula. Tsopano iye anali atakhala ndi Sarah kuyambira pamene iye anali—mtsikana wamng'ono. Iye anali mlongo wake watheka, ndipo iye anali kukhala naye ndipo anamukwatira iye. Ndipo, iye, iye anali nawo. . .Iye anali wosabereka. Iye analibe ana. Ndipo apa iye ali tsopano, iye ali kale. . .ngati iye ali ndi nainte-. . . nainte-naini. Iye ali eyite-naini, zaka eyite-naini zakubadwa. "Koma, Abrahamu, pumula mu chikhulupiriro cha Mawu Anga. Ine ndikukulonjeza iwe, Ine ndidzachita zimenezo. Ndine El Shaddai. Ndine Mulungu wa Mabere kwa ana Anga amene akukhulupirira." Ngati inu simukufuna kuyamwa, chabwino, ndiye musanene kenanso za izo, inu mukuona. Koma ngati iwe uli mwana, iwe ukuyamwa, ukupumula, lonjezo lirilonse!

174 Zindikirani, chikhulupiriro chenicheni chimakhazikika pa thanthwe lolimba la lonjezo la Mawu a Mulungu. Icho sichimasuntha. Chikhulupiriro chenicheni chimazikika.

175 Monga nyenyezi ya kumpoto, nyenyezi ya kumpoto ndi chomangira kwa woyendetsa ngalawa aliyense, kampasiyo imamulozera iye kokha ku nyenyezi ya kumpoto imeneyo. Ndipo Mulungu, Mawu, ndi nyenyezi ya kumpoto ya Mkhristu aliyense, ngati iwe wasochera, ndipo Mzimu Woyera ndi umene umakulozera iwe kwa Iwo. Iwo sumalozera ku china

chirichonse. Timalingaliro tina tonse, ndi zina zotero, ndi—ndi Chikhristu chosakanizidwa mmenemo, chirichonse chimene icho chingakhale; izo ziri ngati dziko, likusuntha, ilo limasintha nyenyezi zimenezo, koma ilo silingakhoze kusintha nyenyezi ya kumpoto. Komanso palibe chirichonse chingasinthe Mawu a Mulungu. Nangula kwa Iwo, khalani nawo Iwo!

176 Tsopano, chikhulupiriro chenicheni sichimasuntha ndi tizikhulupiriro ndi ziphunzitso zopangidwa ndi anthu, ndi kusakhulupirira. Izo zimakhalabe ndi Mawu, chikhulupiriro chenicheni mu Mawu.

177 Ndipo ndi pati pamene inu mungaikepo chikhulupiriro chanu pa china chirichonse kupatula Mawu? Ngati Mulungu ananena izo, gwirani chala chanu kwa Iwo, Iwo ndi owona. Icho sichimasuntha. Icho chimayamwa kuchokera mu Bukhu lapachifuwa cha Mulungu, Baibulo, Zake—zikhumbo Zake, zimene Iye analonjeza. Chimene Iye analonjeza, ndiwo Mawu Ake. Mawu amadzibala Okha. Iwo ayenera kukhala lingaliro lisanakhale Mawu, kenako Mawu; kenako Mawu nkuwonetseredwa, ndipo ndi pamene inu mumayamwirapo zanu—mphamvu zanu kuchokerapo. Kukhulupirira! Kukhulupirira! Kwa Mlengi . . . Kukhulupirira, monga Iye anali, Mlengi amene anapanga dziko lapansi.

178 Chipangano Chatsopano chinati, kumbuyo kuno, "Monga Mose ankakweza njoka mchipululu, chomwechonso Mwana wa munthu ayenera kuti akwezedwe mmwamba." Cholinga chomwecho. Chinali chiyani chimenecho? Iwo anali kumukayikira Mulungu, ndipo matenda ndi mavuto zinadzalowamo. Ndipo anakwezera mmwamba njokayo. Zachiyani? Kwa machiritso awo ndi kukhululukidwa kwawo. Ndicho chimene chinali. Ndipo mkuwa umaimira chiweruzo Chauzimu; ndipo Yesu anali njoka imeneyo yoweruzidwa, ndithudi, mawu akuti mkuwa.

179 Tsopano, Iye atatha kutsimikizira pangano, kapena pangano linawonetseredwa kwa iye, izo zimapereka chikhulupiriro kwa ana owona a Mulungu. Mawu amapereka chikhulupiriro, Mmodzi-Wamabereyo. Izo—izo zimachita chinachake kwa iwo pamene—Mawu, kapena pamene pangano liwonetseredwa, zimapereka chikhulupiriro kwa ana owona a Mulungu.

180 Tsopano ife tikudziwa, ife tikuzindikira kuti, mu izi, Iye ankatchedwa Elohim. Mawu nawonso, pomasulira apa, amatanthauza "Elohim." Ndinangoyang'ana izo, kuti nditsimikizire. Elohim! Ndipo *Elohim* ndi "Mmodzi wokwanira mu Zonseyo." Iye ndi El Shaddai, Elohim, Mulungu-Wamabere, Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo. Iye sasowa kanthu kuchokera kwa wina aliyense. Iye ndiye chikwaniritso chanu chonse.

181 Zindikirani, zomwezo zikuchitiridwa umboni apa, ine ndinali kuzindikira madzulo ano pamene ine ndinali

kuphunzira, mu Yobu, Yobu. Iye akutchedwa "Elohim." Ndipo Yobu ananyozedwa, anasekedwa; momwe, ndi chithunzi bwanji lero. Koma Yobu anali kupumula mu lonjezo la Elohim, "Ngakhale mphutsi za khungu ziwononge thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu, yemwe ine nditi ndidzamuwone kwa inemwini." Kupumula mwa Elohim, ziribe kanthu chimene chingabwere.

182 Mkazi wake anabwera, anati, "Iwe ukuwoneka womvetsa chisoni, Yobu." Ndipo apa panabwera otonthoza ake pamenepo, "Oh, iwe ukuwona zomwe zachitika kwa iwe, mnyamata wokalamba? Ine ndimakuuza iwe kuti ukulakwitsa, nthawi zonse. Wawona zomwe zachitika?" Anthu ambiri amakonda kuponyera pa anthu monga chomwecho.

183 Yobu anali munthu wabwino wa tsiku lake. Munthu wabwino amene Mulungu anali naye padziko lapansi anali Yobu. Iye anamuuza Satana kuti, "Palibe wonga iye." Ameni. "Kodi iwe wamuganizira iye?"

184 Satana anati, "Eya, chirichonse chimabwera mophweka kwa iye. Muswe mpanda umenewo ndipo mundilole ine ndikhale naye iye. Ine ndimupangitsa iye kuti akutukwaneni Inu pamaso Panu." Iye anachita zonse zomwe iye akanatha, koma iye sanakhoze.

Yobu anapumula mu lonjezo limenelo.

185 Anyamata aja anabwera, ndipo anati "Tsopano, tsopano ali kuti Mulungu yense uja amene iwe unali kumukamba? Uh-huh, taonani zimene, iwe—iwe ukumukhulupirira Iye kuti ali ichi, taona—taona zimene zikuchitika tsopano."

186 Koma iye anapumulabe mu El Shaddai, mpaka ziribe kanthu ngati zithupsya zake zinkamuphwasula iye ndipo moyo wake unali ngati wapita. Iye amakhala pa mulu wa phulusa, akukanda zithupsya zake.

Mkazi wake anati, "Iwe . . . Bwanji iwe osatukwana Mulungu ndi kufa?"

Anati, "Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa." Oh, mai!

187 "Ambuye anapereka, ndipo Ambuye atenga, lodala likhale Dzina la Ambuye. Ine ndikudalira mu Elohim. Ngakhale Iye atawononga thupi ili, mphutsi za khungu zitalidya ilo, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu, amene ine ndidzamuwona ndekha; maso anga adzawona, osati wina." Iye anatulukira, mu Mateyu 27, pamene oyera anawuka, anatulukira ndipo analowa nawo, koma kwambiri . . . analowa mu mzindawo. Choyimira chomwecho cha lero, komabe kuyembekezera, kudalira mu lonjezo.

188 Zindikirani Iye atatha kuwonekera mu Dzina ili, Dzina la Mulungu Wamphamvuzonse.

189 Tsopano, mpingo, tsopano ife tikhoza kupeza kachiphunzitso kakang'ono chabe apa, zikhoza kukhala kupotoza pang'ono kwa inu. Ngati inu simukukhulupirira izo, izo ziri kwa inu. Ife basi tiri apa, ine ndingoyankhula zimene ine ndikuganiza. Inu muli nawo ufulu woganiza zomwe inu mukufuna kuganiza.

190 Koma, zindikirani, koma zinthu zonsezi zinali "zoyimira, mithunzi, ndi zitsanzo," monga Baibulo linati izi zinali. Zonsezo ndi chimenecho. Ndipo izi ziri, Mulungu akuchita ndi Abrahamu mu ulendo, chimodzimodzi monga momwe Iye adzachitire ndi Mbewu yachifumu ya Abrahamu mu ulendo. Zindikirani, Iye amachita nawo Ayuda mwanjira yomweyo. Izo zonse zinayambira kumeneko, mu lonjezo limenero la pangano; mafuko onse, anthu onse.

191 Zindikirani kutatha kuwonekera mu Dzina ili la Mulungu Wamphamvuzonse. Ndipo zinawululidwa kwa iye kuti Iye anali Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo. Iye analibe othandizira; Iye samasowa aliyense, alembi aliwonse. Iye anali yekha, Mulungu. Iye anali Mulungu, yekha. Ndipo Iye anawonekera kwa Abrahamu mu Dzina ili, ndipo pamene Iye anawonekera kwa iye mu Dzina ili, ndipo Abrahamu anazindikira Yemwe Iye anali, Iye anasintha dzina la Abrahamu. Tsopano iye wafika ku chidzalo cha kukhulupirira tsopano. Mukuona pamene Mpingo wabwera? Ine ndikuyembekeza inu mukhoza kuwerenga pakati pa mizere. Wabwera pamalo amene Iye wawululira kwa iye Yemwe Iye anali, ndiyeno Iye anasintha dzina la Abraham kuti lonjezo likhoze kukwaniritsidwa.

Tsopano inu mukuti, "Simumakhala kalikonse mu dzina."

192 Ndiye nchifukwa chiyani Iye anasintha dzina la Abraham kuchoka kwa Abram kudzakhala Abraham? Ndi chifukwa chiyani Iye anasintha dzina la Yakobo kuchoka kwa *Yakobo*, "supplanter," kudzakhala *Israeli*, "kalonga ndi Mulungu"? Ndi chifukwa chiyani Iye anasintha dzina la Saulo kudzakhala Paulo? Ndithudi, dzina lake, ndithudi, ndithudi limatanthauza chinachake. Ndithudi limatero. Ngati simunatchulidwe molondola, Mulungu adzalisintha ilo, ngati Iye wakuitanani inu. Inde, bwana.

193 Zindikirani, Iye anasintha dzina lake pano tsopano, kuchokera kwa Abram kudzakhala *Abraham*, chimene chimatanthauza, "atate wa mafuko," anawonjezera h-a-m, Abraham. Chotero Iye anachita zimenezi kuti lonjezo lathunthu likwaniritsidwe. Ndipo mwana tsopano, yemwe anali atalonjezedwa kwa nthawi yayitali, akanakhoza kuwonedwa, kapena, mwinamwake, kuwululidwa, pamene Iye anasintha dzina lake ndipo iye atazindikira Yemwe Iye anali. Iye mwinamwake ayenera kuti anali, mwina ankaganiza kuti panali gulu la iwo; koma iye anazindikira kuti Iye anali Elohim,

Mulungu yekha. Koma, pamene iye anachita zimenezo, ndiye Iye anamusintha dzina lake. Iye anati, "Tsopano, Abraham, iwe sudzatchedwanso Abram, koma *Abraham*, pakuti, 'atate wa mafuko,' Ine ndakupanga iwe." Abraham, tsopano, iye ali mu chikhalidwecho tsopano. Iye ali mu chikhalidwecho pambuyo pa vumbulutso la Yemwe Iye ali. Iye tsopano ali mu chikhalidwe chakuti amuwone mwanayo akuwululidwa.

194 Mwanayo wakonzeka kuti abwere, kuti adzawululidwe. Oh, ana a Abraham!

195 Zindikirani, Iye anasintha dzina la mtumiki Wake, pa nthawi yotsiriza yomwe. Posachedwapa, anali nainte-naini, chatsala chaka chimodzi, ndipo Iye anasintha dzina lake kuchoka kwa Abram kudzakhala Abraham. Kusintha dzina lake, anawonjezera h-a-m, lomwe limatanthauza "atate." Iye anali woti adzakhale atate, atate wa lonjezo; atate, lonjezo.

196 Oh, ngati inu muli nako kuzindikira kwauzimu, mvetserani! Pambuyo pa vumbulutso la Dzina Lake, la Yemwe Iye anali, Iye anasintha dzina lake. Tsopano litachitika vumbulutso, tsopano Iye analikantha dziko lapansi, "palibe gulu la Amulungu; alipo Mmodzi," tsopano ndi nthawi ya vumbulutso la Mwana amene analonjezedwa kuti adzawululidwe kwa Mbewu yachifumu ya Abrahamu, ya lonjezo.

197 Taonani, Iye anazisintha izo kuchokera kwa Wesley, Baptisti, Presbateria, Chipentekoste. Ine sindikudziwa ngati ndinene izi kapena ayi. Inu simukusowa kuti muzikhulupirira izi. Koma ine ndikuyembekeza inu mundikhululukira ine, pakuti ine sindikufuna kuti ndikupwetekeni inu.

198 Koma, taonani, sipanayambe pakhalapo mtumiki kwa mipingo ya—ya Mulungu, kudutsa mu mbiriyakale yonse ya nthawi, yomwe inakhalapo ndi mtsogoleri, chiyambireni kukonzanso, monga mtsogoleri yemwe ife tiri naye lero, Billy Graham, kulondola, chifukwa iye wapita ku dziko lonse. Mukuona? Ndipo, zindikirani, ife sitinayambe takhalapo ndi munthu, wokonzanso aliyense. . . Ife timutenge Sankey, Moody, Finney, Calvin, Knox, aliyense yemwe angakhale, Wesley, Luther, sipanakhalepo mmodzi wa dzina lothera h-a-m, nkale. Mtumiki yekhayo yemwe ife takhalapo naye mmibadwo ya mpingo, ali ndi dzina lothera h-a-m; G-r-a-h-a-m, Graham.

199 Ndipo Graham ndi zilembo sikisi, ndipo sikisi ndi nambala ya munthu, tsiku la munthu; munthu analengedwa, mu—mu Genesis 1:26, pa tsiku la sikisi. Koma seveni ndi chiwerengero cha Mulungu; tsiku la seveni, Mulungu anapuma. Osati sikisi, kusonyeza kuti G-r-a-h-a-m uyu akhoza kukhala kwa mpingo umene uli mdziko; koma, A-b-r-a-h-a-m, Abraham ndi zilembo seveni.

200 Mukuti, “Palibe chirichonse mu manambala.” Ndiye inu simukudziwa manambala a Baibulo lanu. Mukuona? Inu ndithudi mulakwitsa Izo tsopano. Zedidi.

201 Mulungu amakhala “wangwiro” mu *firii*, ndi “kupembedzedwa” mu *seveni*, ndi “kuyesedwa” mu *forte*, ndi “zikondwerero” mu *fifite*, oh, chirichonse chimene inu mukufuna kuchita. Masamu onse, Baibulo limayenda mu masamu.

202 Zindikirani, wa sikisi ndi mtumiki woti atumizidwe ku dziko lapansi. Ndipo, zindikirani, seveni ndi chiwerengero cha Mulungu.

203 Ndipo zindikirani pa nthawi iyi ya kuwonekera tsopano, kapena kuwulula kwa Mwana. Pamene a . . . Izo zidzawululidwa, Mwana. Iwo anali atazindikira kale Dzina Lake, anadziwa Yemwe Iye anali. Iye ndi El Shaddai, Wamphamvuzonse, Elohim. Koma tsopano ife tikufika ku nthawi ya Mwana wolonjezedwa kuti adziwulule Yekha. Mwana, Isaki Mwiniwake yemwe analonjezedwa, wakonzeka kuti abwere powonekera.

204 Ndipo Iye sakanakhoza kuchita izo mpaka Iye atatumiza ndi kusintha dzina lake kuchokera kwa Abram kukhala Abraham, chifukwa, “atate wa mafuko, iye anali.” Zindikirani, *-ham*, h-a-m, “atate, atate wa mafuko.”

205 Tayang’anani momwe izo zikukwanirana ndi Malaki 4, “Kubwezeretsa Chikhulupiriro, kubwerera kwa makolo,” Mbewu ya Abrahamu idzabwezeretsedwa ku mtundu wa Chikhulupiriro chimene atate Abraham anali nacho, Mbewu yake yachifumu. Malaki 4 kuti akwaniritsidwe, ndi kubwezeretsanso Chikhulupiriro chimene chinalipo kale mmbuyomo pachiyambi, kuchibwezeretsanso Icho kwa Mbewu yachifumu ya Abraham. Ndi lonjezo. Ndiro ndendende lonjezo. Mbewu Yachifumu ndi yoti iwululidwe, ndipo mwa . . . mwa Mbewu Yachifumu, imene ili Mbewu Yachifumu, ya Khristu. Khristu ndi Mbewu Yachifumu. Ndipo Mbewuyo ndi Mzimu Woyera umene uli mmitima ya anthu amene amakhulupirira mwa Mulungu, amene akugwira Mawu Ake, ndipo Mulungu akugwira ntchito kupyolera mwa iwo, kunyamula Uthenga womwewo. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silindiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine; Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu. Ndipo ntchito zimene Ine ndikuchita, inunso muzidzazichita.” Mwaona, kuwulula izo mmasiku otsiriza apa, momwe izo zikuyenera kubwerera.

206 Tsopano, penyani mutu wa 18 tsopano. Mwamsanga dzina litasinthidwa, Mulungu akuwonekera, kuti adziwulule Yekha mu thupi. Dzina litapangidwa kudziwika, Yemwe Iye ali, Mulungu akuwonekera mu thupi. Abrahamu, tsiku lina lotentha, masabata angapo chabe kapena miyezi Sodomu

asanawotchedwe ndipo Isaki anabwera powonekera. Ndipo, zindikirani, Abrahamu akukhala pansi pa mgwalangwa wake.

207 Ndipo Loti ali uko mu Sodomu, ndipo iwo akusangalala ndi zosangalatsa za mdziko. Komabe, iye ndi M'busa Loti, mwinamwake iye anali ndi gulu labwino laling'ono kumusi uko. Chirichonse chimene iye anachita, Baibulo linati, "Zoipa ndi machimo a—a nthawiyo anasautsa moyo wake wolungama." Kotero iye ayenera kuti anali ndi ma Loti ambiri amakono lero, koma iye ankadziwa kuti iye sakanakhoza kunena kanthu za izo. Kotero ndiye zindikirani, apo iye anali.

208 Koma Abrahamu, Iye atatha kuwululidwa kwa iye, tsopano, Elohim anali Yemwe anakhala akuyankhula ndi iye. Tsopano iye wakhala pansi pa mgwalangwa, ndipo apa pakubwera amuna atatu, akuyenda ngati anthu. Penyani mphamvu ya vumbulutso, la Yemwe Mulungu anali, linali pa Abraham, chimene ilo linachita kwa iye. Dzina lake litasinthidwa kuchoka kwa Abram kudzakhala Abraham, iye anawona Amuna atatu akubwera, ndipo iye anawatcha atatuwo, Mmodzi, "Mbuye wanga." Atatu a iwo, kukhala Mmodzi. Osati chomwecho ndi nambala sikisi, Loti; iye anawona awiri akubwera, ndipo iye anati, "ambuye anga." Masomphenya a Abrahamu ndi vumbulutso zinamuwonetsa iye kuti Iye anali Elohim Wokwanira mu Zonseyo. Mbewu Yake iyenera kulandira chinthu chomwecho.

209 Zindikirani momwe Iye anadziululira Yekha, momwe Iye anadzipangitsira Yekha kudziwika, kaya iye anali kulondola kapena ayi. Zindikirani, kwa okhulupirira owona, chizindikiro chomwe Iye anachita. Kodi Iye chinamuchitikira chiyani, kuti amupangitse iye kudziwa kuti ameneyo anali Elohim?

210 Tsopano, iye anati, "Mbuye wanga." Ndi chilembo chachikulu A-m-b-u-y-e. Sikolala aliyense, inu mukudziwa izo; sikolala aliyense amadziwa kuti ameneyo ndi Elohim, Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo, Elohim.

Mwamuna ananena kwa ine, nthawi ina, "Inu simumakhulupirira kuti ameneyo anali Mulungu?"

211 Ine ndinati, "Ine ndithudi ndimatero. Abrahamu anati Uyo anali Mulungu. Iye anayankhula ndi Iye; iye ayenera amadziwa." Eya.

212 "Oh," iye anati, "inu mukutanthauza kuti Mulungu atayima pamenepo akudya mnofu wa ng'ombe ija, ndi—ndi kumwa mkaka wochokera ku ng'ombe, ndi kudya mkate wa chimanga, chirichonse chimene inu mukufuna kuchitcha icho pamenepo?"

213 Ine ndinati, "Iye anachita zimenezo. Bwanji, inu simukumudziwa basi Mulungu wathu." Chabwino, mai, Iye akanakhoza basi . . . Bwanji, Iye anangofikirapo . . .

214 Ife tinapangidwa kuchokera ku michere sikisitini; mafuta, kuwala kwa cosmic, ndi potashi ndi kashiamu, ndi zina zotero,

zinthu sikisitini basi. Iye anangozigwira izo pamodzi, ndipo anauzira mwa izo, ndipo anayenda kupita mdziko lapansi. Ndine wokondwa kuti Iye ndi Atate wamtundu umenewo. Ngakhale mphutsi zitawononga thupi ili, komabe Iye adzakuitanani inu. Iye analonjeza kuti Iye adzachita zimenezo. Iye ndi Elohim. Anawuzira zina zodzadza mdzanja, ndipo anati, "Bwera pano, Woodworm," kapena chirichonse chimene chinali, Angelo, "ndipo anapita kumeneko. Tiyeni titsikireko ndipo tikayang'ane ku Sodomu, tikawone chimene chikuchitika."

215 Ndipo Abraham, litachitika vumbulutso, iye analiwona ilo ndipo iye anadziwa kuti panali Mulungu mmodzi. Ndipo iye anaziwona izo, ndipo iye anati, "Ambuye wanga, bwerani pambali, khalani pansi, ndiroleni ine ndisambitse mapazi Anu." Tsopano, iye sananene kuti, "mbuye. . . " Ndipo, penyani, izo ziri mu—izo ziri mu chilembo chachikulu pamenepo. Aliyense akudziwa zimenezo. Ine ndiri ndi Emphatic Diaglott. Mwaona, ndi chilembo chachikulu A-m-b-u-y-e, "Ambuye," Elohim, Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo. Anati, "Ndiroleni ine nditenge madzi pang'ono ndi kusambitsa mapazi Anu, ndi kukupatsani Inu chidutswa cha mkate, ndiye Inu mukhoza kumapita pa njira Yanu."

216 Mukuti, ine ndachedwa kwambiri pano. Ine kulibwino ndifulumire. Ine—ine ndikufuna kufika cha kuno, ndipo ine sindikudziwa kuti ine ndikwanitsa liti. Mungopirira nane motalikirapo pang'ono pokha, inu mutero? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

217 Zindikirani, Elohim, Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo, Mulungu. Ndipo Iye anati . . . Penyani chimene Iye anachita.

218 Tsopano, awiri a Iwo anawuyambapo, iwo anapitirira kumayang'ana mmusi cha ku—cha ku Sodomu.

219 Ndipo Iye anati, "Kodi inu mukuganiza kuti Ine ndingabise chinsinsi ichi kwa Abraham?" Iye samachita kanthu mpaka Iye ataulula izo kwa aneneri Ake. Mwaona, Iye amawadziwitsa iwo. Ndipo Iye anati, "Ine sindimubisira izi, powona kuti iye—iye ndi wodalitsidwa wa Mulungu ndipo iye adzalandira dziko lapansi, ndi zina zotero. Mbewu yake idzakhala, mwinamwake, idzakhala atate wa mafuko ambiri. Ine sindimubisira iye zimenezo. Ine ndimudziwitsa iye zimenezo." Ndipo kotero Iye anati, anayamba kuwulula kwa iye.

220 Ndipo Iye anati, "Abraham," osati Abram. "Abraham, ali kuti mkazi wako, S-a-r-a-h?" Kodi Iye anadziwa chotani zimenezo? Chabwino, basi tsiku izo zisanachitike, iye anali Abram, tsiku kapena awiri izo zisanachitike. Ndipo iye anali Sarai, ndipo tsopano iye ndi Sarah. Ndipo iye ndi Abraham. Anati, "Abrahamu, ali kuti mkazi wako, Sarah?"

Abrahamu anati, "Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu."

221 Iye anati, “Ine ndidzakuchezera iwe molingana ndi nthawi ya moyo. Ndipo mwana uyu yemwe analonjezedwa, wakonzeka kuti abwere powonekera tsopano. Inu mukhala naye iye.”

222 Ndipo Sarah, kwa iyemwini, anakhala ngati anaseka, anati, “Ine pokhala wokalamba, ndipo ndidzakondweranso ndi mbuye wanga, ndipo iye wokalamba?” Chinachake chonga icho, chotero, chifukwa iye anali—iye anali nainte, ndipo iye anali handiredi. “Ndipo tsopano kodi ine ndingakhoze kuchita izo kachiwiri?”

223 Ndipo Mngelo, mtumiki, Mulungu mu thupi la munthu, anati, “Nchifukwa chiyani iye anaseka?”

224 Icho chinali chitsimikiziro. Chifukwa chiyani? Zinasonyeza kuti vumbulutso linali loona. Zinasonyeza kuti chimene iye anamutcha Iye, Elohim, chinali cholondola. Chifukwa, Iye anali Mawu. Icho chinali. . .Mu Ahebri, mutu wa 4, ndime ya 12, anati, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndipo amazindikira zolingirira ndi zokhumba za mtima.” Ndipo pamene Abraham anawona izi, iye anali wotsimikiza ndiye kuti iye akanakhoza kumutcha Iye, “Elohim.” Elohim, Iye anali Mawu, “Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

225 Zindikirani pamene Yesu, Mbewu yachifumu ya Abraham, inabwera powonekera, Iye anadziulula Iyemwini kwa mbewu yachibadwa ya Abraham, mu chizindikiro chomwecho. Ndipo iwo anamutcha Iye, “Belezebule.” Icho chinawachititsa iwo khungu, osakhulupirira, kuwachititsa iwo khungu ndi kuwapangitsa iwo kuchitira mwano, ndi kuwatumiza iwo ku gehena. Koma izo zinapereka kupenya Kwamuyaya kwa okhulupirira, amene anadzozedwera ku Moyo Wamuyaya.

226 Zindikirani, Yesu analonjeza kuti. . .mmasiku otsiriza, kudza kwa Mwana wa munthu kusanachitike, kuti Iye adzabwera ndi kudzadziwulula Yekha, pamene masiku amene Mwana wa munthu ali kuwululidwa, Mbewu yachifumu iyi ya Abrahamu idzawone chizindikiro chomwecho. Tsopano zindikirani, pamene Iye ananena, ndizo—ndizo Luka Woyera 17:28 ndi 30, “Ndipo monga izo zinali mmasiku a Sodomu.” Tsopano, Yesu ananena izi. Ine ndiribe udindo pa zimenezo. Iye. . .Ine ndiri ndi udindo wonena izo, kunena zimene Iye ananena. Koma, Yesu ananena izi, “Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala pa kudza, pa kudza kwa Mwana wa munthu,” tsopano zindikirani, “mmasiku amene Mwana wa munthu akuwululidwa, pamene Mwana wa munthu akuwululidwa ku Mpingo Wake.”

227 Monga kwa Abrahamu. Iye anali Mulungu, Iye anapitiriza kumabwera chotsika; anatsimikizira panganolo, anazindikira Yemwe Iye anali, ndipo dzina lake linasintha. Zindikirani, ilo

linasintha Iye asanafike pa phiri, akuyang'ana pamwamba pa Sodomu, basi Mwana wolonjezedwayo asanabwere.

228 Yesu ananenanso chithunzi chomwecho. Yesu anali kuwerenga Baibulo lomwelo limene ine ndikuwerenga ndipo inu mukuwerenga. Ngati inu mukufuna kuti mudziwe chomwe icho chinali, mubwerere ndipo mukawone zomwe iwo anali kuchita mmasiku a Sodomu. Zindikirani, osati mochuluka kwambiri mmasiku a Nowa (Iye anawauza makhalidwe awo oipa, momwe iwo ankadyera, kumwa, kukwatira, kuperekedwa mu chikwati), koma mu Sodomu.

229 Tsopano pali "palibe madzi," Mulungu analonjeza izo mwa chizindikiro cha utawaleza. Iye anatipatsa ife chizindikiro. Iye nthawizonse amapereka zizindikiro. Utawaleza. . .Iye nthawizonse amakumbukira zizindikiro Zake. Nthawizonse wokhulupirika kwa izo kudutsa zakazi, samalephera kupereka chizindikiro cha utawaleza. Iye nthawizonse amapereka zizindikiro Zake. Zindikirani.

230 Ndipo mu chizindikiro chimenecho, Iye analonjeza kuti sadzawononga dziko lapansi "osatinso ndi madzi," koma Iye ananena kuti ilo lidzatero "lidzayaka." Ndipo zindikirani Yesu apa akunena, "Monga zinali mmasiku a Sodomu," dziko la Amitundu linali loti lidzawonongedwa. Achisodumu!

231 Tsopano tayang'anani pa makhalidwe a mafuko. Tayang'anani pa makhalidwe a mpingo, monga ngati Loti. Taonani zomwe ziri pansi pakati pawo: mwamuna, G-r-a-h-a-m, kuwakankhira iwo kutali, andale amenewo, kwa mpingo mwachibadwa. Tsopano pa mpingo wauzimu. . .

232 Nthawizonse pamakhala magulu atatu a anthu. Ndiwo, okhulupirira, osakhulupirira, ndi odzipangitsa-kukhulupirira. Iwo amakhala nawo mu gulu lirilonse. Ngati inu munamverera kupyinjika kumene ine ndinachita, inu mukanadziwa kuti iwo anali pano usikuuno. Kotero ndiye, kotero, inu. . .ndi atatu onse. Zindikirani, ndi inu pamenepo, nthawizonse pamakhala makalasi atatu amenewo kulikonse.

233 Tsopano ngati mungawone kuti izo zinali zoti zidzakhala chinthu chomwecho pamene Mwana wa munthu anali woti adzawululidwe kwa Mbewu yachifumu ya Abrahamu, kudzera mwa Khristu (Khristu ndi Mbewu Yachifumu), pamene Iye akuwululidwa mmasiku otsiriza. Tsopano, mwapamalo, dziko likukhala ndendende, chifukwa Mwana amene anawuka Kummawa akudzalowa Kumadzulo. "Ndipo ilo linali tsiku lachimbuuzi," anapanga mabungwe, zipembedzo, "koma kudzakhala Kuwala mu nthawi yakumadzulo," anatero mneneri Yeremiya. Tsopano, ndipo mmasiku pamene Mwana ameneyo, Iye akutuluka kuchokera kuseri kwa mitambo ya chipembedzo, kuti adzadziwulule Iyemwini, Iye anati dziko lidzakhala litakhala monga momwe linakhalira mmasiku a Sodomu,

ndipo Mwana wa munthu adzadziulula Yekha kachiwiri kwa anthu Ake. Taonani momwe Iye anaululira izo kwa mbewu ya Isaki; yang'anani momwe Iye ati adzawululire izo kwa Mbewu yachifumu, Mkwatibwi Wachifumu, Mfumukazi. Mfumukazi ndi Mbewu yachifumu.

234 Monga Mulungu anatulutsira fuko kuchokera ku fuko, mu Igupto, Iye akutulutsa Mpingo kuchokera mu mpingo, kapena Mkwatibwi kuchokera mu mpingo; Mpingo kuchokera mu mpingo. Ndipo otsalira a Mbewu ya mkazi, ndi amene anatsalira, "padzakhala kulira ndi kuchita ukali ndi kukukuta kwa mano, chifukwa iwo analibe Mafuta mu nyali zawo, Mzimu Woyera," nthawizonse umaimirira. Ndi zimenezotu pamenepo.

235 Malowo akukhala bwino bwino. Ndipo tsopano yang'anani pamwamba pa phirilo. Tsopano, Mpingo, Abrahamu; Loti; achi Sodomu. Dziko; mpingo; Osankhidwa. Mpingo, Mkwatibwi, kuchokera mu mpingo. Ife tikukhala pamalo mokhoza. Dziko liri mu kutembenuka koyenera kwa ilo.

236 Kupotoza! Chirichonse chapotozedwa. Ndizo, ine ndidzakuuzani inu, chirichonse ndi haibridi. Iwo . . .

237 Ine ndimabwera kuno, ndinawona chikwangwani chachikulu, chinati, "Chimanga cha haibridi." Bwanji, icho si chabwino. Ayi. Izo ziyenera kukupangitsani inu osakhulupirira kuti mulumphe. Pamene Mulungu anati, "Mulole mbewu iliyonse ibale mwa mtundu wake." Ndipo inu mukhoza kupanga chimanga cha haibridi ndi kuchipanga icho kukhala chimanga chowoneka bwino, koma inu simungakhoze kuchibzalanso icho kachiwiri; mulibemo moyo mwa icho.

238 Ndipo umo ndi momwe ife tachitira ndi tchalitchi. Ife tachipanga icho kukhala chokongola, ndipo tachikongoletsa icho ndi zonyezimira zachipembedzo, koma icho chiribe Moyo mwa icho. Icho sichingakhoze kubala umboni wa Baibulo umenewo kachiwiri. Mukuona? Sichingakhoze kubala umboni wa chiwukitsiro cha Khristu. Ndi nkhani ya haibridi.

239 Anthu ovala bwinoko, olipidwa bwinoko, zipembedzo zokulirapo, olemera, a M'badwo wa Laodikaya, ndendende. "Olemera, osasowa kanthu; osadziwa kuti ndiwe omvetsa chisoni, watsoka, ndi wakhungu, ndi wosauka, wamaliseche, ndipo osadziwa izo." Ngati munthu akanadziwa kuti iye ali maliseche, inu mukanakhoza kumuyankhula iye. Koma pamene iye sakudziwa izo, amenewo ndi mawonekedwe omvetsa chisoni, omvetsa chisoni. Musawanyoze anthuwo, koma muziwachitira chifundo. Bwanji ngati ameneyo mukanakhala inu mu chikhalidwe chimenecho? Bwanji ngati Mawu akanati sanawululidwe kwa inu, kodi inu mukanachita chiyani? Ndi chiyaninso chikanakhala chofunikira, ngati maso anu akanakhala akhungu kwambiri inu simukanakhoza kuwawona Iwo? Awo ndi mawonekedwe omvetsa chisoni.

240 Ndipo ndendende basi, mwapamalo. Inu simungakhoze kuika chala pa icho; apo icho chakhala, basi zomwe Iye ananena kuti zikanadzachitika. "Zizindikiro izi zidzakhala mmasiku otsiriza." Onani pamene iwo akhala, basi ndendende.

241 Tsopano penyani, kupanga haibridi. Inu mukudziwa, ngati chirichonse ine. . .Inu mutenge, monga inu mutenge b—b—b—bulu, ndi kumubereketsa iye kwa kavalo, kavalo wamkazi, kani, ndipo kodi inu mumapeza chiyani? Inu mumapeza mphongolo. Koma mphongolo ameneyo sangakhoze kuberekanso kachiwiri. Mukuona? Mulungu anati, "Mulole mbewu iliyonse ibale za mtundu wake." Tsopano kodi kusintha kwanu kumachokera kuti? Ntchito yanu yomwe yatsutsa chimene inu munanena kuti inu mumakhulupirira. Mulungu anati, "Mulole mbewu iliyonse ibale mwa mtundu wake." Iyo siyingakhoze kuberekanso kachiwiri. Ayi, ayi. Iyo yatha.

242 Ndipo ine ndikuganiza mphongolo ndi imodzi ya—zinthu zaumbuli zomwe ine ndinayamba ndaziwonapo. Inu simungakhoze kumuphunzitsa iye kalikonse. Iye adzakhala pamenepo ndi makutu akuluakulu aatali awo, inu mukudziwa, ndipo iye adzadikirira mpaka miniti yakufa yomwe kuti akukankhe iwe, iye asanafe. Iye basi . . .

243 Inu simungakhoze kumuphunzitsa iye kalikonse. Izo zikundikumbutsa ine. . .Iye adzakhala pamenepo, ndipo inu mupite mukamuuze iye zinthu, zikundikumbutsa ine za anthu ena, akudzinenera kukhala okhulupirira lero. Makutu aakulu aatali, atakhala pamenepo, ndipo, "Masiku a zozizwitsa anapita. Hoo! Hoo! Hoo!" Iye sakudziwa kumene iye anachokera. Iye samadziwa kanthu za Iwo. Chinthu chokhacho chimene iye amachidziwa ndi kachikhulupiriro kena ka mpingo.

244 Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu, ine ndiri ndi ulemu kwa mtundu wamba. Mnyamata, iye akhoza kukuuzani inu mtundu wake. Iye akhoza kukuuzani inu omwe anali abambo ake, omwe anali amayi ake, omwe agogo ake aakazi, agogoamuna anali. Iye ndi mtundu weniweni.

245 Chomwechonso amatero Akhristu enieni amenewo, akhoza kuziyendetsa izo molunjika kumene ku Bukhu la Machitidwe ndi kuwona kumene iwo anachokerako, Mkhristu wamtundu weniweni, wobadwa mwa Mzimu womwewo, chinthu chomwecho, kumachita mwanjira yomweyo.

246 Ndi ozunza omwewo; abulu ndi akavalo akudyera pamodzi. Ndiko kulondola. Ndi zimenezotu pamenepo. Inu muyenera kukhala nazo izo, ngakhale. Lero ndi tsiku la haibridi.

247 Ine ndinawona nkhani mu *Reader's Digest,* osati kale litali, "Pitirizani kudyetsa akazi nyama ya haibridi iyi ndi—ndi zinthu, iwo sangakhoze kukhala ndi ana awo. Iwo akusintha. Iwo akumakula mmapewa, ndipo akumachepa mchiuno." Bwanji,

ndicho, inu mukudziwa munthu nthawizonse amadziwononga yekha ndi chitukuko.

248 Bwererani kwa Mulungu! Khulupirirani Mulungu. Bwererani ku Mbewu yapachiyambi. Bwererani ndipo mukhulupirire Iwo. Inu munawerengapo te anga . . . inu muli nawo matepi anga, kani, ine ndikuganiza munawamverapo iwo, pa: *Mbewu Yapachiyambi*, ndi *Mtengo wa Mkwatibwi*, ndi zinthu zimenezo, zomwe ziri zoona. Ambuye akudziwa zimenezo.

249 Momwe zinthu zimenezo zimanenedweratu, miyezi ndi miyezi. Anthu inu, zomwe inu mukuwona pano, ndi zazing'ono chabe, zomwe inu mukuwona zikuchitika. Afunseni anthu omwe akhalapo, afunseni ngati nthawi imodzi zinayamba zalepherapo. Umafotokoza za anthu, zivomezi, zinthu zomwe ziti zidzachitike. Mzimu Woyera umatiuza ife. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."] Pali munthu amene wakhalapo . . . Zedi. Ndi anthu osiyanasiyana.

250 Monga Marilyn Monroe, kale asanamwalire. Iwo ananena kuti iye anadzipha. Iye sanachite zimenezo. Iye anamwalira ndi nthenda ya mtima. Mwamtheradi.

251 Munthu uyu, wankhondo uyu. Maginot Line ku Germany. Zinthu zonsezo, basi masauzande a zinthu, mwangwiro pa dontho, nthawi iliyonse. Iwo sangakhoze kukhala china chirichonse koma Mzimu Woyera. Mukuona? Mukuona? Iye analonjeza izo.

252 Iye anapereka zinthu seveni mu 1933, zomwe zidzachitike. Ndipo tsopano chimodzi chirichonse cha izo chafika pochitika koma zinthu ziwiri, mwangwiro, basi ndendende. Momwe kuti ngakhale Purezidenti Kennedy adzatengedwera mkati. Izo ziri mmenemo pa mabuku anga pakali pano, zonenedwa zaka sate-firii zapitazo, ndendende. Momwe kuti Mzere wa Maginot udzamangidwire, zaka leveni iwo usanamangidwe. Momwe Hitler akanati adzawukire, ndi—ndi Fascism, ndi—ndi Nazism, ndi zonsezo kuti zidzamangire mu chikominisi, ndipo chikominisi chidzawononga Chikatolika. Ndipo icho chidzatero, inde, ziribe kanthu zomwe iwo akuchita. Ndipo anasonyeza, anati padzakhala Bungwe la Ecumenical, ndi momwe mipingo yonse ikanati idzabwere pamodzi ndi kudzapanga fano lotchedwa Chilemba cha Chirombo. Inu mukumawawona iwo pa msewu pomwe, pakali pano. Ndendende kulondola. Izo ziyenera kuchitika, chifukwa izo sizimalephera kukhala ziri.

253 Aliyense amene amadziwa konse zimenezo, aliyense, zitengeni izo kuzungulira dziko lapansi, izo sizinalepherepo nthawi imodzi. Miyezi ndi zaka kutsogolo kwa nthawi, izo zimangokhala zolondola mwangwiro pa dontho. Ndi Mulungu pakati panu, anthu; Mulungu ali mwa ife, Mzimu Woyera. Zindikirani, Yesu ananena kuti Mbewu yachifumu

idzazindikiridwa ndi chinthu chomwecho, apa mu Luka mutu wa 17. “Oh, bwererani, O omwazika, kuchoka ku zipembedzo zanu, kupita kwanu.”

254 Aliyense wa ife akhoza kukhulupirira kuti Mulungu... Ngati inu mumakhulupirira mwa Mulungu, inu mukudziwa kuti Mulungu amachiza odwala. Ilo si funso. Bwanji, ngati inu simukukhulupirira zimenezo...Inu mukudziwa, iwo ankanena mmasiku amenewo, “Yehova, ife tikudziwa Iye akhoza kuchiritsa, koma Iye sangathe kupulumutsa.” Tsopano, “Iye akhoza kupulumutsa, koma Iye sangakhoze kuchiritsa.” Mwaona, basi mdierekezi yemwe yemweyo, chinthu chomwecho. Iye ali zonse Mpulumutsi ndi mchiritsi. Iye ndi Yehova-Yire ndi Yehova-Rafa.

255 Oh, bwererani! Kumbukirani, Iye analonjeza malo awa, a chirichonse chitakhala momwe izo ziriri tsopano, za zomwe ziti zidzachitike. Iye anati izo zidzachitika, ndipo izo ziyenera kuchitika.

256 Anthunu, ine ndikupepesa. Ine ndakusungani inu mochedwa tsopano. Tiyeni tiweramitse mitu yathu miniti yokha, ine nditero...Ine ndidzatsiriza izi, mwinamwake, mawa usiku. Ine ndiri nawo pafupifupi masamba ena sikisi a zolemba pano. Muweramitse mitu yanu mphindi chabe. Mukhale olemekeza, aliyense.

257 Inu mukhoza kusagwirizana ndi ine; inu muli nawo ufulu kwa zimenezo. Ine ndiri nawo ufulu wofotokoza zomwe ine ndikuganiza. Ine ndinali nalo Lemba. Tsopano, ziribe kanthu zomwe ine ndinganene, ngati Mulungu saikira kumbuyo izo, ndiye Urimu Tumimu sikugwira ntchito, ndiye iyo yakanidwa. Ziribe kanthu momwe izo zikumvekera zabwino, ndi momwe izo zikumvekera zenizeni, Urimu Tumimu ayenera kuzisonyeza izo. Mbewu iyenera kubwera ku moyo. Ngati iyo siyitero, ndiye kuti iyo siyinali chomwecho.

258 Tsopano, kwa machiritso, ine ndayesetsa kukuuzani inu kuti ine sindine mchiritsi. Alipo anthu ambiri amene amadzitcha okha achiritsi. Ndiye alipo ambiri—otsutsa omwe amawatcha anthu achiritsi, zimenezo, kungofuna kuti awatsutse. Mtima wawo suli paubwenzi ndi Mulungu. Mukuona? Aliyense amadziwa kuti palibe munthu angachiritse mzake. Mulungu amachiza matenda. Mulole Mulungu ayitanire imfa yanu, ndipo mupemphere zonse zomwe inu mukufuna, ndipo chipatala chimakupatsani inu jakisoni wa mankhwala tsiku ndi tsiku, ndipo inu mudzafa chimodzimodzi basi.

259 Ngati ndingadule dzanja langa usikuuno, ndi kudzayima pano ndi dzanja lodulidwa, palibe mankhwala padziko lapansi omwe angachiritse dzanja langa. Ife tiribe mankhwala amene amachiritsa. Palibe mankhwala amene amachiritsa. Dokotala aliyense angakuuzeni inu zimenezo. Iwo amangotsukapo

pamene Mulungu amachiritsa. Iwo sangakhoze kumanga minyewa. Ngati ndingadule dzanja langa, ndipo, "O," inu mukuti, "inde, M'bale Branham, alipo mankhwala ochiza zimenezo." Chabwino, ine ndikufuna kudziwa ndi ati amenewo.

260 Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu. Ngati nditadula dzanja langa ndi kugwa pansi wakufa apa, dokotala akhoza kubwera ndi kudzakonza thupi langa ndi kupangitsa kuti ine ndiwoneke mwachibadwa kwa zaka fifite. Kulisoka dzanja langa, ndi kunditengera ine kunja uko ndi kumakandibaya jakisoni wa penicillin, tsiku lirilonse, ndipo mu zaka fifite kuchokera tsopano kuchekeka kumeneko kudzakhala monga momwe zinaliri pamene iko kunapangidwa. Ngati—ngati mankhwala anapangidwa kuti azichiritsa pochekeka, bwanji iwo samachiritsa zimenezo? Mankhwala aliwonse amene angachiritse kuchiritsa kuchekeka pa dzanja langa, adzachiritsa kuchekeka pa desiki iyi, adzachiritsa kuchekeka pa chikhoto changa. Ngati iwo angachiritse kuchekeka, iwo akhoza kuchiritsa kuchekeka ziribe kanthu pomwe iko kuli. "Chabwino," inu mukuti, "bwanji, mankhwala anapangidwira anthu." Ndiye bwanji iwo samachiritsa? "Chabwino," inu mukuti, "moyo wachoka mwa inu." Ndiye kuti pali chinanso pambali pa mankhwalawo chimachiza.

261 Ndi moyo, zedi, ndipo moyo ndi Mulungu. Ndithudi, izo ndi choncho. Komabe, ena ndi ochimwa, apotozedwa nazo izo, komabe inu muli mu chifanizo cha Mulungu. Ndipo moyo umene inu muli nawo umene Mulungu anaupereka iwo kwa inu. Inu mukudziwa zimenezo; ayi, chifukwa Mulungu ndiye mchiritsi. Moyo ndi mchiritsi. Inu mukukhulupirira zimenezo, mwaona. Ndawona zambiri zikuchitika!

262 Tsopano tiyeni tingomuvomereza Iye, sichoncho inu? Ife tisanachite zimenezo, ine ndikudabwa ndi angati muno amene akhutitsidwa, kale. . .Ngati ndinu obwera kumene kuno, simunayambe mwakhalapo muno kale, kuti inu mukumukhulupirira Iye kuti ndi Mwana wa Mulungu? Ndipo mwa ichi, Uthenga usikuuno, Mawu okha, Iye asanachite nkomwe chirichonse, kuti inu mukhulupirire Iwo, ndipo inu mukufuna kuti ine ndikukumbukireni inu mu pemphero, kwezani mmwamba dzanja lanu. Mutero inu? Oh! Mulungu akudalitseni. Oh, mai! Manja firii kapena foro handiredi. Mulungu akudalitseni inu.

263 "Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva kwa Mawu." Chifukwa chimene ine ndinanena zimenezo, Mbewu idzapeza chisomo ndi Mulungu. Ine ndikuganiza tsopano, mmalo mwa—mwa kungoyitana mzere wa pemphero pamwamba pano, ine ndingokupangani inu kuti mupemphere.

264 Ndiroleni ine ndikupatseni inu Lemba, poyamba. Ndi zimene ife timachita, ziyenera kukhala Mwamalemba. Ziyenera kukhala

Mwamalemba! Mulungu sadzalemekeza china chirichonse. Mulungu sadzalemekeza bodza; inu mukudziwa zimenezo. Inu—inu simungakhoze kuziyika izo kwa Iye. Iye samalemekeza mabodza. Iye amangolemekeza kokha Mawu Ake. Koma Iye analonjeza, kuti, “Mawu Anga sadzabwerera kwa Ine pachabe. Iwo adzakwaniritsa zomwe Iwo anakonzedwera.” Ndipo ife tikuwona Mawu omwe anaikidwira kwa lero. Ziribe kanthu kuchuluka kwa kusakhulupirira kowuka mu msasa, Mulungu adzalemekeza Mawu Ake pamene Iye apeza chikhulupiriro choti awalemekeze nawo Iwo.

265 Tsopano penapake mchipinda chino, ine ndikufuna inu mutenge Lemba ili. Ahebri mutu wa 3, ine ndikukhulupirira ndi umenewo. Baibulo linanena kuti, kuti, “Iye ndi Wamkulu Wansembe, pakali pano, amene akhoza kukhuzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu.”

266 Ndipo inu amene munakweza dzanja lanu, ine ndikufuna inu, mwamsanga pamene msonkhano ukufika kumapeto apa, ine ndikufuna inu mubwere ndi kudzayima mozungulira pano ndipo mudzapempherereredwe, kumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanu. Mudzatege ulendo wopita ku chimodzi cha tchalitchi chabwino kuzungulira kuno. Ziribe kanthu komwe icho chiri, winawake amene amalalikira Uthenga, mupite kwa iwo ndipo mukapemphe ubatizo wa Chikhristu. Ndipo abusa adzakutengani inu kuchokera pamenepo nkumapitirira. Iye ndi munthu wa Mulungu. Iye anaitanidwa kuti adzakhale munthu wa Mulungu, iye adzatero—iye adzakutengani inu kuchokera pamenepo nkumapitirira. Basi, ngati ine ndikanamakhala mu mzinda uno, ine ndikanakhala wa yina ya mipingo iyi kuno. Ine ndikanabwera kwa iwo, iwo amene amakhulupirira Uthenga. Ine ndikanakhala kumeneko. Ndithudi, ine ndikanazidzindikiritsa ndekha ndi iwowo, chifukwa ndicho chimene inu muyenera kuchita. Ndipo ndicho chimene inu mukuyenera kuchita.

267 Tsopano, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemwe angakhoze kukhudzidwa ndi zomverera za zifooko zathu, tsopano Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, chotero Iye ayenera kuti achite mofanana monga Iye anachitira dzulo.

268 Tsopano penyani, mkazi wamng'ono anakhudza chovala Chake, nthawi ina, ndipo Iye anatembenuka ndipo anadziwa chimene iye anali nacho, ndipo anamuuza iye kuti chikhulupiriro chake chinamupulumutsa iye. Ndipo iye anamverera, mwa iyemwini; iye sanatenge kupweteka kulikonse kuti atsimikizire izo. Iye sankasowa kuti atsimikizire izo.

269 Inu simumatsimikizira zinthu. Inu mumakhulupirira Mulungu. Mukuona? Inu simumatsimikizira Mulungu, nkomwe. Inu simungakhoze kutsimikizira, kuti mupulumutse moyo wanu,

alipo Mulungu, kungopita kunja kuno ndi kukati, "Ndiroleni ine ndimuwone Iye." Mwaona, inu muyenera kumukhulupirira Iye.

270 Zida zonse za Mulungu ndi zauzimu. Chikondi, chimwemwe, chikhulupiriro, kupirira motalika, chipiriro, kufatsa, mwaona, zonsezo zauzimu. Ife timayang'ana pa zinthu zimene iwe sungathe kuziwona ndi diso lako lachibadwa.

271 Ndipo Khristu ali pano usikuuno. Iye analonjeza izo. "Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, pamenepo Ine ndiri pakati pa iwo. Pamenepo Ine ndidzakhalapo!" A "Ine" kachiwiri, Iye ali pano. Tsopano, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

272 Inu muzipemphera, ndi kumati, "Ambuye Yesu, ine ndikudwala," kapena chirichonse chimene inu mukuchifuna. "Ine—ndine wosowa, ndipo ine—ine ndikufuna Inu, Mulungu wokondedwa, kuti mundichitire ine chifundo, ndipo mundichiritse ine ndipo mundipange ine kukhala bwino. Ndipo tsopano ngati ine ndiri ndi chikhulupiriro chokwanira, Ambuye, kuti ndikukhudzeni Inu. . .Ine—ine ndikudziwa kuti M'bale Branham samandidziwa ine. Ndine mlendo. Ndipo ine ndikudziwa kuti iye sakundidziwa ine. Tsopano, ngati—ngati munthu ameneyo wandiuza ine Choonadi, chimene ine ndikukhulupirira icho chiri, chifukwa icho chikuchokera kumene ku Mawu Anu. Ine ndachiwerenga Icho, ine ndikuwona Icho chikuwoneka cholondola mwangwiro basi. Tsopano mutsimikizire Icho. Ine ndimadzinenera kuti ndine Mbewu ya Abrahamu, kudzera mwa Khristu, ine ndimadzinenera kuti ndine Mbewu yachifumu, kukhulupirira pa Yesu Khristu, Mbewu Yachifumu. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ndine gawo la Mkwatibwi Wake, Mpingo Wake umene Iye akuwudzera. Ndipo ine ndikudwala komanso ndikusowa. Chonde, Ambuye Yesu, ndiloleni ine ndikhudze chovala Chanu. Ndipo con-. . .ndipo mutsimikizire izo kwa ine poyankhula kupyolera mwa M'bale Branham, monga Iye analonjezera izo zikanadzakhala 'monga izo zinali mmasiku a Sodomu.' Mungondilora ine. . .mumulole iye andiuze ine zomwe ine ndikuganiza, kupempherera, zomwe ine ndikufuna, zomwe zosowa zanga ziri, chinachake chokhudza ine." Inu muzichita zimenezo, ingochitani izo.

273 Atate Akumwamba, tsopano zonse ziri mmanja Mwanu. Tsopano izi ndi zonse zomwe ine ndingakhoze kuchita, kapena munthu wina aliyense, angakhoze kungonena zomwe Inu mwanena *Pano*, Choonadi. Tsopano zitsimikizireni izo, Ambuye, kuti ndi Choonadi. Ine ndayankhula za Inu. Yankhulani kuti ine ndanena Choonadi. Mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

274 Ine ndikufunani inu basi—kuti mungokhulupirira, mungokhala ndi chikhulupiriro. Tsopano pasakhale mmodzi

woyendayenda. Mungokhala molemekeza kwenikweni. Ine ndikufuna inu mulingalire kuimirira pamaso panu, mkati muno penapake, Khristu, woukitsidwa kwa akufa; anabwera kupyola makoma nthawi ina, anadya mkate, anati, "Ndikhudzeni Ine, Ndine mnofu ndi mafupa," ndipo anasowa pamaso pawo pomwe. Tsopano Iye—Iye analonjeza kuti Iye akanadzawonekera mmasiku otsiriza, mmawonekedwe a thupi la munthu kachiwiri, mu thupi lanu, monga Iye anachitira mmasiku a Sodomu. Mulungu, yemwe anali Khristu, atawonetseredwa mthupi, tsopano ali mu Mpingo Wake, Mkwatibwi Wake. Mwaona, iwo akubwera pamodzi. Ndi nthawi yolumikizana. Mipingo ikulumikizana, mafuko akulumikizana, ndipo Mkwatibwi ndi Khristu akulumikizana. Mwaona, ndi nthawi yolumikizana.

275 Tsopano mungokhulupirira, mophweka. Musayesere kuchita manjenje ndi kukanikiza chinachake, chifukwa inu simupeza kalikonse. Basi—basi modzichepetsa nenani, "Ambuye, ine ndikukhulupirira." Winawake angochita zimenezo. Ndipo tsopano ine. . .

276 Ndi angati akhala patsogolo panga, makamaka. . . Tsopano, ine ndikuwadziwa amuna awa *pano*, ndi awa *apa*. Ndikudziwa ena akhala *pano*. Nanga bwanji pomwe *pano*, patsogolo panga pomwe? Tiyeni tipatulire pa gulu laling'ono ili pomwe *pano* penapake. Ndi angati amene sanayambe amuwonapo Khristu akudzidziwitsa Yekha chotero, mwa. . . Tiyeni tiwone manja anu, "Sindinayambe ndaziwonapo izo." Ine ndikuganiza aliyense waziwonapo izo. Chabwino.

277 Inu mupemphere tsopano. Tsopano mungokhala molemekeza. Ine sindikudziwa kuti Iye atero. Ine sindingakhoze kunena zimenezo. Izo ziri kwa Iye. Kodi izo zikupangitsani inu kukhulupirira, mwamphamvu kwenikweni? Ambuye amamva zimenezo. Iye amadziwa zinthu zonse.

278 Mwamuna wakhala apo pomwe, akuvutika ndi mwela. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza mwela imeneyo? Inu mukutero? Ndife alendo kwa wina ndi mzake, ine ndikuganiza, inu ndi ine. Ine sindikukudziwani inu. Ine sindinayambe ndakuwonanipo inu. Koma ngati ndicho chimene inu munali kuchipempherera, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, bambo uyu wakhala. . .

279 Kodi inu mukukhulupirira zimenezo—kodi inu mukukhulupirira kuti pamene Andireya anamuuza Simoni kuti abwere adzawone kuti iwo anali atamupeza Mesiya, ndipo pamene iye anabwera mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu. . .? Pokhala kuti inu mukukhudzana ndi Chinachake tsopano, pemphero lanu. Mwaona, Iye anamuuza iye yemwe iye anali. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Ngati inu muti mukhulupirire zimenezo, Iye akhoza

kuchita zimenezo. Kodi zimenezo zingakulimbikitseni inu kuti mukhulupirire ndi mtima wanu wonse? Kodi izo zingachite ndi inu nonse mwanjira imeneyo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

280 Tsopano bamboyo wakweza manja ake mmwamba, kuti chirichonse chimene anauzidwa iye. . . Ine sindikudziwa; Ine ndiyenera ndikamvetsere tepiyo, mwaona. Chirichonse chimene icho chinali, chinali cholondola. Ndi kulondola uko, bwana? [M’baleyo akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino. Chirichonse chimene icho chinali, ndi cholondola.

Bambo Shepherd, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. “Ngati inu mungakhoze kukhulupirira.”

281 Tsopano izo siziri zambiri kuposa zomwe Iye ananena, “Dzina lako ndiwe Simoni, mwana wa Yonasi.” Tsopano ngati inu mungokhulupirira, ndizo zonse zomwe ziri zofunikira. Mukuona? Tsopano ndi chiyani icho? Iye analonjeza zimenezo. Iye anapereka lonjezo limenelo. Izo zikusonyeza kuti Iye ali pano. Osati ine ndekha; Iye ali mwa inu. Iye ali mu Thupi Lake la okhulupirira.

282 Dona wamng’ono, akulira ndipo akupemphera, mutu wanu wawerama. Mukuvutika ndi khansa. Ngati simuchita mantha, ndipo mukhulupirira, Mulungu akuchizani inu ngati inu mungakhulupirire izo. Iye achiphonya icho, ndithudi. Akazi a Hood, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano, kuti Yesu Khristu wakuchizani inu, ndipo inu mukhoza kukhala nacho chimene inu mwachipemphacho. Tsopano inu mukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse? Ameni.

283 Wakhala pafupi ndi inu pali dona yemwe ali ndi vuto la mmimba, vuto la mtima, zosokonezeka. Ngati mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kulandira machiritso anu. Kodi inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse, kodi inu muvomereza izo? Inu mutero? Chabwino.

284 Bambo uyo pamenepo ali ndi zotupa, kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza zotupa zimenezo ndi kukupangani inu kukhala bwino? Imirirani.

285 Kodi inu mukuganiza chiyani za zimenezo, mwakhala pafupi ndi iye pamenepo, muli ndi mwela? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuchiza mwela imeneyo ndi kukupangani inu kukhala bwino?

286 Dona pafupi ndi nkono wanu apo, akuvutika ndi mutu. Izo zapita tsopano. Sichoncho inu? Mwaona, chikhulupiriro chanu chinachita zimenezo. Ndizo zonse zomwe inu muyenera kuchita, ndi kungokhulupirira.

287 Apa pali dona yemwe ali ndi matenda a shuga. Inu mukukhulupirira Mulungu akuchizani inu, dona, mwakhala pamenepo ndi matenda a shuga? Inu mukukhulupirira Mulungu

akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Inu mukutero? Akazi a Robinson. Ndiro dzina lanu.

288 Muyike dzanja lanu pa iye pamenepo chifukwa cha mwela imeneyo, mwinamwake Mulungu amuchiza iye, nayenso. Ngati inu mukukhulupirira zimenezo! Kodi inu muchita zimenezo? Chabwino, bwana.

289 Dona wakhala pafupi ndi inu, ikani dzanja lanu pa iye, bwana, iye ali ndi dzanzi. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza dzanzi ndi kukupangani inu kukhala bwino? Inu mukutero, inu mukhoza kulandira machiritso anu, inunso. Inu muyenera kukhulupirira izo.

290 Tsopano ndicho chitsimikiziro. Mulungu anapanga lonjezo, tsopano ndi angati akukhulupirira kuti Khristu ali pano? Inu mukukhulupirira zimenezo? Tsopano, nonse a inu amene mukufuna, mu Kukhalapo Kwake tsopano, amene mukufuna chifundo kuchokera kwa Iye, amene mukufuna chifundo pa solo yanu, ndipo inu mukufuna kuti mumulandire Iye tsopano pamene inu muli mu Kukhalapo Kwake komwe, kuzindikiridwa. Tsopano ine. . .

291 Munthu akhoza kubwera muno ali ndi zipsyera za misomali mmanja mwake, ndi kukhulika kwa minga ndi kudzanena kuti, "Ine ndine Ambuye." Wachinyengo aliyense wakale akhoza kuchita zimenezo. Koma, Moyo! Thupi la Ambuye Yesu likukhala kudzanja lamanja la Ufumu; pamene Iye abwera, nthawi idzakhala kulibenso, pamene thupi limenelo lidzabwerera ku dziko lapansi. Koma Mzimu Wake uli pano, Moyo Wake ukupereka umboni wa Iye kukhala pano. Mukuona? "Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezero a dziko lapansi."

292 Ndipo inu mukufuna chifundo kuchokera kwa Iye tsopano, kodi inu mungangoima kwa mawu a pemphero? Paliponse mchipinda muno, inu amene. . .paliponse pamene inu muli, kodi inu mungaimirire? Mulungu akudalitseni inu, mmbuyo uko. Ndiko kulondola, ingoimiriranі. Ingoimirirani pa mapazi anu, ndizo zonse zomwe ine ndikufuna kuti inu muchite. Ingoimirirani miniti, kwa pemphero. Ngati inu mungaimirire mmalo mwa Iye! Ngati mukuchita naye manyazi Iye tsopano, Iye adzachita nanu manyazi pamaso pa Atate; ndipo ngati ndinu—ngati mukulolera kuti mumuvomereze Iye tsopano, Iye adzakuvomerezani inu pamaso pa Atate. "Ine tsopano ndikufuna kumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanga. Ine ndikufuna kuti Iye andidzaze ndi Mzimu Wake pakali pano. Ine ndikumufuna Iye." Ingokhalani chiimire kwa mphindi yokha, kwa pemphero, ngati inu mungathe. Imirirani. Uko nkulondola. Ine ndikufuna. . .Ine ndikumverera kutsogozedwa kuchita izi, kupanga gu-. . .Uku ndi kuyitanira ku guwa. Imirirani. Ife tiribe guwa loti mubwereko; mtima wanu

ndiro guwa. Mungokokera mmbuyo kusakhulupirira konse, ndi kudziwa kuti Iye ali pano tsopano. Muimirire pa mapazi anu, inu amene mukufuna kumulandira Khristu pakali pano, mu Kukhalapo Kwauzimu kumene inu mukukumverera, kumene kwatsimikiziridwa tsopano.

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu.

293 Ambuye Yesu, iwo ndi Anu. Inu munati, "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye." Ndipo tsopano molingana ndi sayansi, iwo sakanakhoza ngakhale kukweza dzanja lawo; lamulo la mphamvu yokokera pansi limati manja athu ayenera azilendewera pansi. Koma muli moyo mwa iwo, ndipo moyo umenewo unabweretsedwa pafupi ndi Moyo Wamuyaya, Khristu. Ndipo iwo anapanga chigamulo mu mtima mwawo, kuti iwo athana nalo dziko lapansi. Ndipo iwo akweza manja awo ndipo aimirira pa mapazi awo, kunyoza lamulo la mphamvu yokokera pansi, kuti muli moyo mmenemo. Chomwechonso ife tikunyoza lamulo la dziko lapansi ndi kusakhulupirira!

294 Mu Dzina la Yesu Khristu, iwo ndi Anu. Iwo ndi mphatso za chikondi za Uthenga. Izo ndi zikumbutso za Uthenga, usikuuno, ndi . . . Kukhalapo Kwanu kwakukulu ndi ife. Ikani maina awo pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, Pamenepo, Ambuye. Ife tikupemphera kuti—kuti aliyense wa iwo akakhale Kumeneko, monga ana Anu, okondedwa Anu.

295 Adzazeni iwo ndi Mzimu Woyera wa Mulungu, mmitima yawo. Mulole miyoyo yawo ipatsidwe mphamvu kwambiri ndi Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse, kuti kudzichepetsa ndi chikondi ndi kukoma mtima ndi chifatso ziyenderere kuchokera mwa iwo, ndi changu choona ena akupulumutsidwa, chomwe nthawiyina chinali mu chikhalidwe chawo. Perekani izi, Ambuye.

296 Chinthu chokhacho chimene ife tingakhoze kuchita, Ambuye, ndicho kukhulupirira. Ndipo iwo anayima ngati chikumbutso cha chikhulupiriro chawo. Ndipo tsopano ndi chikhulupiriro changa ndi chikhulupiriro chawo, limodzi, ife tikuziyika izo pa guwa Lanu, mwa chikhulupiriro. Ndipo iwo ndiwo nsembe imene yagona pamenepo, ikuyembekezera Mwana wa Mulungu woperekedwa nsembe kuti awalandire iwo mu Ufumu Wake. Perekani izi, Ambuye. Tsopano mulole iwo akhale Anu, mu Dzina la Yesu Khristu.

297 Tsopano inu amene mukukhulupirira pa Iye ndi mtima wanu wonse, amene mwaimirira, kwezani mmwamba dzanja lanu, nenani, "Ine ndikumukhulupirira Iye. Ine ndikumulandira Iye pakali pano ngati Muwomboli wanga, ndipo ine ndikufunafuna ubatizo wa Mzimu Woyera." Kwezani dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu.

Tsopano inu mukhoza kukhala pansi.

298 Ndipo ine ndikufuna inu mupange ulendo wanu wopita ku tchalitchi china, tsopano, pomwepo.

299 Mawa usiku ife tidzakhala ndi a—msonkhano wa ubatizo wa Mzimu Woyera, mawa usiku, pomwe pano mchipinda. Tsopano, pali zotengeka zambiri zomwe iwo amadzitcha ubatizo wa Mzimu Woyera, koma izo sizikutanthauza kuti kulibe Mzimu Woyera weniweni. Kuli Mzimu Woyera weniweni wa Mulungu, mofanana basi. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Iye adzakomana nafe ife kuno mawa usiku.

300 Tsopano, ndi angati mchipinda muno ali okhutitsidwa kuti ife tiri pa nthawi yotsiriza? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndi angati akukhutitsidwa kuti ichi ndi Choonadi, Mawu akuyenera kukhala mwanjira iyi mmasiku otsiriza? Kwezani dzanja lanu. ["Ameni."] Ndi angati a inu omwe muli okhulupirira? Baibisani manja anu. ["Ameni."] Chabwino. Yesu ananena Mawu awa, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira, ngati inu muli wokhulupirira."

301 Tsopano ndi angati amene mukusowa Khristu mu thupi lanu? Kwezani mmwamba manja anu. Chabwino, inu okhulupirira amene mwakhala pafupi ndi iwo, ikani manja anu pa wina ndi mzake. Ndipo momwe inu mumapempherera mu tchalitchi chanu, umo ndi momwe inu muzipempherera kuno. Musadzipempherere nokha. Inu muwapempherere iwo; iwo akukupempharerani inu. Ndipo Baibulo linati, "Iwo adzayika manja pa odwala, iwo adzachira." Tsopano mupemphere momwe inu mumachitira, ndipo ndi lonjezo.

302 Ambuye Yesu, iwo ndi Anu. Alandireni iwo mu Ufumu Wanu. Ndipo mumuchize aliyense, Ambuye; ndi mipango iyi. Mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, perekani izi, Ambuye. Satana wataya kugwira kwake. Mulole Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse imuchize aliyense.

64-0403 Yehova-Yire #2
4-H Club Barn
Louisville, Mississippi U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.


Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:


VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org